Stephanos

# Umoyo wacikristu

1. Baibulo
2. Thanzi ndi matenda
3. Cuma ndi umphawi
4. Mdima ndi Kuunika
5. Pemphero
6. Coonadi ndi cinyengo

## Malangizo a aphunzitsi

- Inu aphunzitsi muyenera kuzindikira kuti kuli nkhondo pakati pa Mulungu ndi Satana. Mulungu afuna anthu kudziwa coonadi. Satana afuna kunyengerera anthu. Ndipo nkhondo iyi ndi ya nthawi zonse. Pamene muphunzitsa muyenera kukhala okonzeka kuthana ndi zinthu izi za uzimu (Aefeso 6.10-18).
- Aphunzi ena angakhale anthu amene amaphunzitsa ziphunzitso zonama. Ena angakhale anthu amene ananyengeredwa. Pemphani Mulungu nzeru kuti mulankhula nao.
- Phunzitsani momveka. Osagwiritsa mabodza. Khalani okoma mtima ndi odekha pamene muphunzitsa coonadi ca Mulungu: sitifuna anthu kulakwiridwa cifukwa ca njira m'mene aphunzitsidwa. Aonetseni zoonadi za m'Baibulo ndipo aloleni kusankha zimene afuna kutsata.
- Limbikitsani aphunzi kuwerenga Baibulo kuturukiramo zimene Mulungu akamba. Ngakhale maphunziro athu ayenera kuyesedwa ndipo ali olamulidwa ndi Baibulo.
- Maphunziro atiphunzitsa za *umoyo* <u>wacikristu</u>. Kopanda Yesu monga Mpulumutsi wathu sitikhoza kukhala ndi umoyo wacikristu ndipo sitikhozanso kuona ndi kumvetsa zimene Mulungu afuna ife kudziwa. Cifukwa cace tsindikani m'phunziro lirilonse cofunikira ndi cotheka ca kukhala oyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa Yesu Kristu.

Cotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yace. Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi – Aefeso 6.10 ndi 11

**Phunziro 1 Baibulo**

<u>Zofunikira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko


## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani onse.
- Fotokozani kuti m'maphunziro awa tidzaphunzira za Cikristu ca masiku onse.
- Maphunziro onse amangidwa pa zimene Baibulo liphunzitsa.

<u>Zidziwitso</u>
- Phunziro lirilonse lidzayamba pa nthawi ya …………. koloko. Fikani pa nthawi yake cifukwa tikacedwa sitidzakhala ndi nthawi yokwanira.
- Ndi cofunikira kwambiri kubwera ku maphunziro onse.
- Aphunzi ayenera kubwera ndi Baibulo ku maphunziro onse. Tilifuna pa nthawi ya kuphunzira.
- M'phunziro lotsiriza tidzalemba mayeso (mphunzitsi adzasankha ngati mayeso adzalembedwa). Kulemba mayeso sikudzakhala bvuto ngati mudzaphunzirako maphunziro onse.

<u>Malamulo</u>
- Ana sadzaloledwa pa nthawi ya maphunziro (makanda adzaloledwa ngati sasokoneza aphunzi).
- Osayenda-yenda pa nthawi ya kuphunzira.
- Khalani bwino ndipo mverani bwino aphunzitsi anu. Khalani omasuka.

- Pemphani Mulungu dalitso pa phunziro iri.

## 2. Ndondomeko ya m'Baibulo, mfundo 1-6 (30 minutes)
- Funsani aphunzi kuti ncifukwa ciani tiyenera kudziwa zimene Mulungu atiuza m'Baibulo. Yankho: Awerengereni <u>2 Timoteo 3.15-17</u>. Fotokozani kuti mwa Baibulo tikhoza kudziwa Yesu Mpulumutsi ndiponso kuphunzira mokhalira miyoyo yathu ya kwa Mulungu.
- Funsani aphunzi kuchula mabuku a m'Baibulo.
- Fotokozani kuti m'Baibulo muli zigawo ziwiri: Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano. Zipangano izi ziwiri ndizo Mau a Mulungu. Komabe, Cipangano Cakale cisiyana ndi Cipangano Catsopano.
- Lembani mzere yoima cambali pa bolodi. Fotokozani ndondomeko ya m'Baibulo mwa kulemba pa bolodi cithunzi ici colembedwa munsi.




1. **Mabuku oyamba a m'Baibulo ndiwo mabuku asanu amene afotokozera njira imene Mulungu anafuna anthu ake Aisrayeli kukhala m'mgwirizano naye.**
   *Genesis, Eksodo, Levitiko, Numeri, Deuteronomo.*

2. **Mulungu analenga bwino zinthu zonse ndi anthu onse** (Genesis 1 ndi 2). Pamene Mulungu analenga zonse, anthu onse anali ndi mtendere ndi Iye, onse anali ndi mtendere ndi anzao ndiponso onse anali ndi mtendere ndi cilengedwe cina conse. Mulungu ndiye Mwini wa zonse. Cifukwa cace tiyenera kumumvera.

3. **Anthu anasankha kusamvera Mulungu**: Adamu ndi Hava anacimwa. Ife tsono tikhala m'ubwenzi woonongeka ndi Mulungu, ife mwini, anthu ena ndiponso ndi cilengedwe cina. Sitidziwerengabe monga Mulungu afuna ife kukhala. Mgwirizano wa ife ndi anthu ena ndiwo woonongeka. Cifukwa cace anthu amalimbana, amadana, amacitana nkhanza, amadziganizira ndi zina zotere. Tilephera kukhala m'mgwirizano ndi cilengedwe. Tingaononge cilengedwe kuti tipindule. Tiyenera kuthana ndi matenda ndi imfa.

4. **Mwa cifundo Mulungu analonjeza kutuma Mpulumutsi kuyanjanitsa zonse zoonongeka** (Genesis 3.15). M'Genesis 3.15 Mulungu anauza njoka kuti kudzakhala ndeu (udani). Ici sicitanthauza cabe kuti anthu adzada njoka. Citanthauzanso kuti kudzakhala ndeu pakati pa Satana ndi Mulungu: Satana adzayesa kuononga anthu (monga njoka iluma citende ca anthu) koma Mulungu adzatuma Mpulumutsi kugonjetsa Satana (ngati mutu wa njoka yalalika citanthauza kuti yafa ndipo ilibe mphamvu konse). Mpulumutsi uyo ndi Yesu Kristu (tikawerenga Luka 3.23-28 tidzapeza kuti Yesu anabadwa m'banja limene liri m'badwo la Adamu ndi Hava).

5. **Zinthu zambiri zinacitika, koma Mulungu anasunga fuko la Israyeli monga anthu ake, iwo angakhale anali ndi macimo ndi mabvuto ambiri.** Izi zonse ndizo mbiri.
   *Yoswa, Oweruza, Rute, 1 Samueli, 2 Samueli, 1 Mafumu, 2 Mafumu, 1 Mbiri, 2 Mbiri, Ezara, Nehemiya, Estere.*

6. **M'Mabuku a ulakatuli tiwerenga za anthu ndi zokhudza zao.** Ici citanthauza kuti m'mabuku awo tiwerenga za zokhudza za uzimu za anthu a Mulungu m'zocitika zosiyana-siyana.
   *Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki, Nyimbo ya Solomo.*

## 3. Kukambirana (15 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu a anthu atatu kapena anai. Apatseni mpata kukambirana ndi kuyankha mafunso awa:
  - Kodi mneneri ndi munthu wotani?
  - Kodi nchito ya mneneri ndi yotani?
- Kambiranani pamodzi. Funsani mafunso ambiri kuti mudziwe ndi kumvetsetsa zimene aphunzi aganiza za aneneri a m'Baibulo ndi a masiku ano.

## 4. Ndondomeko ya m'Baibulo, mfundo 7-17 (60 minutes)

7. **Aneneri anaphunzitsa anthu za Mulungu, chimo ndi cipulumutso.** Iwo anaitana anthu kulapa ndipo mobwereza-bwereza analankhula za lonjezo la Mulungu kutuma Mpulumutsi kuwayanjanitsa ndi Mulungu.
   *Yesaya, Yeremiya, Maliro, Ezekieli, Danieli, Hoseya, Yoweli, Amosi, Obadiya, Yona, Mika, Nahumu, Habakuku, Zefaniya, Hagai, Zekeraiya, Malaki.*
   Kuli zoona zina zimene zikhudza aneneri onse a m'Baibulo:
   - **Analankhula m'malo mwa Mulungu amene analankhula nao mosabvuta** (Yeremiya 1.2, Ezekieli 3.16-17, Hoseya 1.2 ndi Yoweli 1.1).
     Masiku ano tiri ndi Baibulo ndipo tidziwa mosakaika kuti Baibulo ndilo Mau a Mulungu. Mulungu alankhula nafe mwa Yesu Kristu ndipo tiwerenga mau ake m'Baibulo (Ahebri 1.1). Cibvumbulutso ciriconse, ciphunzitso ciriconse ndi ciganizo ciriconse ciyenera kuyesedwa monga za m'Baibulo. Ngati citsutsa ndi zimene Baibulo liphunzitsa, cibvumbulutsoco, ciphunzitsoco kapena ciganizoco ciyenera kukanidwa.
   - **Anaphunzitsa m'mene Aisrayeli anayenera kuyankha cisamaliro capadera ca Mulungu** (Ezekieli 16.1-43, Yeremiya 7.3-11, Amosi 4.6-11 ndi Yesaya 1).
     Aneneri anasonjeza kuti Mulungu akonda anthu ake ndiponso kuti awasamalira. Udindo wa Aisrayeli unali kumtumikira ndi kumumvera Mulungu koma iwo analephera kucita tero: anatumikira milungu ina, sanamvere malamulo a Mulungu, anakana kulapa ndipo sanacite zolongosoka. Udindo wa mneneri unali kusonyeza macimo awa ndi kuitana Aisrayeli kulapa (Yeremiya 35.15).
   - **Iwo anacenjeza kuti kudzakhala ciweruzo coononga ca macimo onse** (Yesaya 2.12-22, Yoweli 2.1-11, Zefaniya 1.7-18).
     Nthawi zambiri ciweruzo ca Mulungu cichedwa *Tsiku la Yehova.* Nthawi zambiri pamene aneneri analosera za tsogolo, iwo analankhula za *Tsiku la Yehova*. Anauza Aisrayeli zimene zidzacitika iwo akapitiriza kucimwa ndiponso zimene zidzacitika iwo akalapa macimo ao. Colinga ca kulosa cinali cakuti anthu aitandiwa kulapa ku macimo ao.
   - **Anaphunzitsa za lonjezo lacifundo la Mulungu la kukonzedwanso ndi kuyanjanitsidwa mwa Mpulumutsi wozunzika ndi womwalira** (Yesaya 9.1-7, Yesaya 11.1-16, Yeremiya 31.31-40, Ezekieli 36.22-32).
     Mpulumutsiwo adzakhala Mkhalapakati amene abweretsa Aisrayeli ndi anthu akunja (si Ayuda) kwa Mulungu mwa Mzimu Woyera. Kupyolera mwa Mpulumutsi kudzakhala kuyeretsa macimo ndi ciyembekezo ca kukonzedwanso kwa kumwamba ndi dziko lapansi. **Mpulumutsiyo wolonjezedwa ndiwo Yesu, Mwana wa Mulungu!** Zonse zimene aneneri analosera za Mpulumutsi zinakwaniritsidwa m'moyo wa Yesu. Awerengereni ndime izi:
     1. Yesaya 7.14 ndi Mateyu 1.20-23 – Yesu adzabadwa mwa namwaliya.
     2. Mika 5.2 ndi Mateyu 2.1-6 – Yesu woweruza adzabadwa m'Betelehemu.
     3. Yesaya 53.7 ndi Mateyu 27.12-14 – Yesu anakhala cete Iye angakhale ananyozedwa.

4. Zakariya 13.7 ndi Marko 14.27 ndi Marko 14.50 – Ophunzira adzathawa pamene Yesu atengedwa kapolo. Yesu anasiyidwa kukazunzidwa.

Ngati aphunzi afuna zitsanzo zina, mungawawerengere: Zakariya 9.9 ndi Mateyu 21.4-7, Yesaya 53.1 ndi Yohane 12.37 ndi 38 ndiponso Hoseya 1.11 ndi Mateyu 2.13-15.

8. **Yesu anabadwa.** Ndico ciyambi ca Cipangano Catsopano. Timakumbukira kubadwa kwake pa tsiku la Krisimasi.

9. **Mabuku anai oyambirira Cipangano Catsopano achedwa Uthenga Wabwino**.
*Mateyu, Marko, Luka, Yohane*
Mabukuwa saphunzitsa za kubadwa kwa Yesu cabe, komanso za:
    10. **Imfa ya Yesu** (Tsiku Lacisanu Loyera) kuyanjanitsa anthu ocimwa ndi Mulungu mwa kukhululukira macimo ao. Iye anaikidwa m'manda.
    11. Patapita masiku atatu **Yesu anauka kwa akufa** (Tsiku la Paska)
    12. Patapita masiku makumi anai (40) **Yesu anabwerera Kumwamba** (Tsiku la Kukwera kwa Yesu).

13. Buku la Macitidwe a Atumwi liyamba ndi nthano ya **kutumidwa kwa Mzimu Woyera** (Tsiku la Pentekoste, masiku khumi patapita Tsiku la Kukwera kwa Yesu). Mzimu Woyera analonjezedwa, Yesu asanapite Kumwamba (Yohane 14.26, Yohane 16.7). Mzimu Woyera anaphunzitsa anthu kulapa macimo ao ndi kukhulupirira Yesu Mpulumutsi.

14. **Zina za m'buku la Macitidwe a Atumwi zitiuza kuti kukula kwa Mpingo Wacikristu watsopano kunali kotani**.

15. **Makalata olembedwa ndi anthu osiyana-siyana kuphunzitsa Akristu za kukhulupirira ciani ndiponso za kukhalira bwanji umoyo.**
*Aroma, 1 ndi 2 Akorinto, Agalatiya, Aefeso, Afilipi, Akolose, 1 ndi 2 Atesalonika, 1 ndi 2 Timoteo, Tito, Filemon, Ahebri, Yakobo, 1 ndi 2 Petro, 1 ndi 2 ndi 3 Yohane, Yuda.*

16. **Buku lotsiriza la m'Baibulo litiuza zimene zidzacitika Yesu asanabwerenso.**
*Cibvumbulutso*

17. **Masamba otsiriza a m'Baibulo atiuza kuti kumwamba ndi dziko lapansi zidzakonzedwanso.** Anthu a Mulungu okhululukidwa ku macimo ao adzakhala naye Kumwamba muyayaya. Anthu ena onse adzakhala ku Gehena muyayaya.

## 3. Kupumula (10 minutes)

- Ngati aphunzi afuna, aloleni kusewera sewero pa nthawi ya kupumula. Pangani magulu atatu. Auzeni lembo, mwacitsanzo lembo 'a'. Lolani gulu lirilonse kupereka maina ambiri oyambira ndi lembo 'a'. Apatseni pointsi imodzi pamene achula dzina lopezeka m'Baibulo.

## 4. Kuwerenga Baibulo – kusiyana kwa Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano (30 minutes)

- Fotokozani kuti Baibulo ndilo Buku lapadera limene lifunika ife kuchereza pamene tiliwerenga kapena kulimvera. Kudziwa kusiyana kwa Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano kutithandiza kumvetsetsa bwino Baibulo.
- Fotokozani kusiyana uku kwa Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano:
    a. Ife monga Akristu a Cipangano Catsopano sitiuzidwabe kusunga malamulo ena a m'Cipangano Cakale, mwacitsanzo malamulo a kupereka nsembe.

M’Cipangano Cakale Mpulumutsi Yesu analonjezedwa. Mulungu anafuna Aisrayeli kukumbutsidwa mosalekeza za cofunikira ca Mpulumutsi. Cifukwa cace Iye anauza kucita miyambo ina yosonyezera Yesu. Mwacitsanzo kupsereza nsembe ya nyama yosonyezera cikhululukiro. M’Cipangano Catsopano atadza Yesu, anthu sanauzidwebe kusunga malamulo a m’Cipangano Catsopano okhudza kupereka nsembe (mwacitsanzo m'Ahebri 10.11-18 m’mene Paulo anafotokozera kuti Yesu anafa kamodzi kukhululukira macimo ndipo cifukwa cace kupereka nsembe si kofunikirabe).

b. <u>Nthawi zambiri m’Cipangano Cakale dalitso la Mulungu ndilo looneka ndi maso ndi la zathupi koma m’Cipangano Catsopano dalitso la Mulungu ndilo losaoneka ndi maso ndi lamuyaya.</u> M’Cipangano Cakale Mulungu ankaonetsa ubwino wake kwa Aisrayeli ndi mafuko okhala pafupi nao mwa madalitso ooneka ndi maso (kutukuka, thandizo, kubereka, thanzi, citetezo, kukolola kwabwino). Cifukwa cace tiwerenga za mgwirizano wa kusamvera ndi kutukuka m’Cipangano Cakale (mwacitsanzo m’Deuteronomo 28 ndi Levitiko 26). Madalitso ooneka ndi maso anagwiritsidwa nchito kukopa mitima ya anthu kuti akhale m’modzi wa Aisrayeli kutumikira ndi kulemekeza Mulungu.

M'Cipangano Catsopano tiwerenga nthawi zambiri za madalitso auzimu kuposa madalitso ooneka ndi maso. Madalitso ooneka ndi maso sabvomerezeka m’Cipangano Catsopano. Monga mwa Cipangano Catsopano, Mulungu amadalitsa anthu ake makamaka ndi madalitso auzimu ndi amuyaya, mwacitsanzo kupezeka kwa Mulungu, cipulumutso, cikhululukiro, umoyo wosatha ndi Mzimu woyera wokhala m’okhulupirira (mwacitsanzo Aefeso 1.3-14).

M'Cipangano Cakale anthu kunja kwa Israyeli anayenera kukopedwa kuti akhale a Aisrayeli kutumikira Mulungu. Koma tsono m’Cipangano Catsopano, udindo wa anthu a Mulungu ndiwo kupita ndi kuphunzitsa amitundu yonse kuti Mulungu ndi Mulungu wa mitundu yonse osati wa Aisrayeli cabe (cifukwa cace: madalitso ooneka ndi maso sapatsidwabe ndi colinga kukopa anthu). Mulungu afuna anthu ake kuphunzitsa Uthenga wa Yesu kuti mphamvu yake idzaoneka mwa kudalitsa anthu ndi madalitso a kuomboledwa ndi kuyanjanitsidwa. Izo ndi zimene tiyenera kuyembekeza ndi kufunsa Mulungu, osati madalitso ooneka ndi maso poyamba, ngakhale Mulungu akhoza kutidalitsa ndi madalitso ooneka ndi maso ngati afuna kucita tero.

- Cifukwa cace, ngati tifuna kudziwa zimene Baibulo liphunzitsa za mfundo zina, tiyenera kudziwa zimene Baibulo liphunzitsa za mfundozo m’mbali ina ya m’Baibulo. Ngati tigwiritsa nchito ndime imodzi cabe pa kulalikira kapena kuphunzitsa, ndi capafupi kunena cinthu cotsutsana ndi ndime zina za m’Baibulo.

## 5. Kuwerenga Baibulo – kuwerenga mau ena anzake – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)

*Pa mbali iyi tidzawerenga ndime zophunzitsa za cuma ndi kutukuka. Osaphunzitsa mozama koma phunzitsani cabe ndime izi ndi zitanthauzo zao cifukwa tidzaphunzira zina zambiri za mfundo izi m’phunziro 2.*

- Ngati tifuna kudziwa zimene Mulungu anena m’ndime yoikika kuwerenganso mau anzake kutithandiza bwino kwambiri. Zitsanzo zina:
  1. Awerengereni aphunzi <u>Mateyu 6.33</u>.
     - Afunseni kuti ndime iyi itanthauzanji.
     - Fotokozani kuti nthawi zambiri ndime iyi yagwiritsidwa nchito kuphunzitsa kuti Akristu obadwa mwatsopano (ndiwo opezeka m’Ufumu wa Mulungu) adzakhala ndi ciriconse cimene afuna.
     - Tsono werengani <u>Mateyu 6.31-34</u>.

- Fotokozani citanthauzo ca Mateyu 6.33 mogwiritsa nchito mau anzake opezeka m'ndime za 31, 32 ndi 34. Mulungu akamba kuti anthu ake sayenera kudera nkhawa cifukwa ca cakudya ndi zobvala koma ayenera kuyang'anira Iye. Akamba kuti adzawasamalira. 'Kukhala ndi cakudya ndi zobvala' kusiyana ndi kulemera!
  Werengani bwino kwambiri: Baibulo likamba za zonse zimenezo zofanizira zinthu zopezeka m'ndime ya 31. Citanthauza kuti sitidzasowa cakudya ndi zobvala. Sicitanthauza kuti zina zonse zimene tingalake kukhala nazo zidzatipatsidwa.

2. Awerengereni aphunzi Agalatiya 6.7.
   - Afunseni kuti ndime iyi itanthauzanji.
   - Fotokozani kuti nthawi zambiri ndime iyi yagwiritsidwa nchito kutiphunzitsa kuti tikapereka, Mulungu adzatipereka mphoto mwa kutipatsa zambiri zoposa: 'Bzalani mbeu!'
   - Tsono werengani Agalatiya 6.8.
   - Fotokozani citanthauzo ca Agalatiya 6.7 mogwiritsa nchito mau anzake opezeka m'ndime ya 8: Mulungu akamba za madalitso amuyaya osaoneka ndi maso, osati za cuma. Ici citanthauza kuti tikakhala miyoyo yathu mwa Mzimu Woyera wotitsogolera tidzakhala m'mene Mulungu afuna ndi kucita zokondweretsa zake. Mphoto yathu idzakhala umoyo wosatha pafupi naye Kumwamba.
3. Awerengereni aphunzi 2 Akorinto 8.9.
   - Afunseni kuti ndime iyi itanthauzanji.
   - Fotokozani kuti nthawi zambiri ndime iyi yagwiritsidwa nchito kuphunzitsa kuti anthu a Mulungu afunika kukhala olemera.
   - Tsono werengani 2 Akorinto 8.7-9.
   - Fotokozani citanthauzo ca 2 Akorinto 8.9 mogwiritsa nchito mau anzake opezeka m'ndime za 7 ndi 8. Mulungu akamba za kucurukira ca cikhulupiriro, mau, cidziwitso, khama, cikondi ndi cisomo. Ndime iyi siyenera kugwiritsidwa nchito kusonyeza kuti anthu a Mulungu afunika kulemera.

- Tsirizani pa kubwereza kuti tikawerenga Baibulo tifunika kukhala ocenjera kuti tisawerenge ndime pa yekha kopanda kuwerenganso mau anzake. Cofunika kwambiri ndi kuwerenga mosamala. Ngati siticita tero ndife osokeretsedwa msanga.

## 6. Kutsiriza (5 min)

- Fupikitsani zimene zaphunzitsidwa lero: Tikafuna kumvetsetsa zimene Mulungu atiuza mwa Baibulo tiyenera kuwerenga mosamala, kuwerenga bwinobwino Baibulo ndi ndime za m'Baibulo. Tifunika kumvetsetsa kusiyana kwa Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano. Cofunikira koposa ndico kupemphera pa kuwerenga kapena kumvera Baibulo, pakuti ndi Mulungu amene atithandiza kumvetsetsa Mau ake.
- Pempherani.

**Phunziro 2 Thanzi ndi matenda**

Zofunikira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro lotsiriza: Tikafuna kumvetsetsa zimene Mulungu atiuza mwa Baibulo tiyenera kuwerenga mosamala, kuwerenga bwinobwino Baibulo ndi ndime za m'Baibulo. Tifunika kumvetsetsa kusiyana kwa Cipangano Cakale ndi Cipangano Catsopano. Cofunikira koposa ndico kupemphera pa kuwerenga kapena kumvera Baibulo, pakuti ndi Mulungu amene atithandiza kumvetsetsa Mau ake.

## 2. Ciyambi ca matenda (30 minutes)
- Funsani aphunzi kuti ncifukwa ciani anthu adwala: kodi kudwala kucokera kuti?
- Fotokozani kuti Mulungu analenga zonse. Analenga zonse bwino. Kunalibe wodwala. Koma Adamu ndi Hava, anthu oyamba pa dziko lapansi, anacimwa: sanamvere Mulungu pa kudya cipatso coletsedwa. Zotsatira zake:
  - Ubwenzi wa Mulungu ndi ife ndiwo woonongeka. Ndife olekanitsidwa ndi Mulungu cifukwa ca macimo athu ndi mitima yathu yocimwa.
  - Ubwenzi wa mwa ife tokha ndiwo woonongeka. Sitidziwerengabe m'mene Mulungu afuna ife kukhala. Anthu ena acita ndi kuganiza monga iwo ndiwo Mulungu. Anthu ena sadziwerengerabe ofunikira.
  - Ubwenzi wa ife ndi anthu ena ndiwo woonongeka. Cifukwa cace anthu alimbana, adana, acitanirana nkhanza, adziganizira ndi zina zotere.
  - Ubwenzi wa ife ndi cilengedwe cina ndiwo woonongeka. Tilephera kukhala m'mgwirizano wabwino ndi cilengedwe. Tingaononge cilengedwe kuti tipindule. Tiyenera kuthana ndi matenda ndi imfa.

- Ciyambi cacikulu ca kudwala ndico chimo loyamba ku Paradaiso. Kucokera pa nthawi iyo zonse ndi zoonongeka ndipo tingadwale cifukwa ca ziyambi zosiyana-siyana (monga tidzaphunzira m'Kuwerenga Baibulo). Si kuti nthawi zonse matenda ndiwo matemberero a Satana ofunika kumasulidwa!

## 3. Kuimba (10 minutes)
- Aphunzitseni nyimbo, mwacitsanzo 'Muthange mwafuna' kapena 'Yang'anani kwa Ine'.

## 4. Zimene Baibulo likamba za matenda – Kuwerenga Baibulo (90 minutes)
*Zoyambitsa mabvuto*
- Werengani Yobu 2.7 ndi Yohane 9.1-3 ndipo yankhani mafunso awa.
  1. **Kodi zoyambitsa matenda ndi mabvuto ndi ziti monga mwa ndime izi?**
     Yankho: Kungakhale zoyambitsa zosiyana-siyana. Coyambitsa cingakhale chimo la munthu mwini (Yohane 5.14), Satana (Yobu 2.7), makhalidwe athu (1 Petro 4.15) ndiponso cingacokera kwa Mulungu amene acigwiritsa nchito ndi colinga (2 Mafumu 15.5, Yohane 9.1-3). Cherezani kuti Mulungu ndi wabwino ndipo sacita coipa ciriconse,

koma akhoza kugwiritsa nchito coipa m'njira yomkomera Mulungu ya ku ulemerero wake. Sitinganene kuti aliyense amene adwala agwiridwa ndi Satana kapena ciwanda!

2. **Kodi tingapeze bwanji ciyambi ca mabvuto m'miyoyo yathu?**
   Yankho: Tiyenera kusinkhasinkha za m'umoyo wathu ndi kumfunsa Mulungu ngati kuli cinthu cimene Iye afuna kutionetsa. Osagwiritsa nchito njira zosaloleka, monga kupita ku ng'anga (Deuteronomo 18.9-14). Osayesa kupeza ciyambi ca mabvuto a anthu ena pakuti ndi cinthu ca pa yekha. Nthawi zina sitingokhoza kudziwa coyambitsa (monga Yobu). Siyani zonse kwa Mulungu.
3. **Tingayankhe bwanji anthu amene anena kuti Mulungu salola anthu ake kudwala?**
   Yankho: Si zoona. Nthawi zina sitingamvetsetse Mulungu. Akhoza kugwiritsa nchito matenda ndi mabvuto ku ulemerero wake. Mkhulupirireni pa nzeru zake ndi mphamvu yake.

*Kubvutika ndiko mbali ya Cikristu*

- Werengani pamodzi Afilipi 1.29 ndi 2 Timoteo 3.12 ndipo yankhani funso iri.

4. **Kodi mungayankhe bwanji anthu amene anena kuti Akristu obadwa mwatsopano azikhala opambana ndi athanzi?**
   Yankho: Mulungu amathandiza ndi kusunga anthu ake (Yesaya 43.2) koma ici sicitanthauza kuti iwo sangabvutike. Kubvutika ndiko mbali ya kukhala Mkristu (2 Timoteo 3.12, Macitidwe 14.22, Macitidwe 20.22-24). Mulungu akhoza kugwiritsa nchito mabvuto kuphunzitsa anthu ake (Ahebri 12.6-10). Baibulo litiuza za okhulupirira okhulupirika amene anadwala (Trofimo (2 Atimoteo 4.20), Lazaro (Yohane 11.3), Elisa (2 Mafumu 13.14), Epafrodito (Afilipi 2.25-27), Tabita/Dorika (Macitidwe 9.37)). Baibulo siwaikira mlandu pa kudwala ndi kubvutika.

- Werengani pamodzi Yesaya 53.3-5 ndipo yankhani mafunso awa.

5. **Kodi ndime izi zilankhula za yani?**
   Yankho: Zilankhula za Ambuye Yesu amene anazunzika ndi kumwalira pa mtanda.
6. **Kodi colinga ca imfa ya Yesu pa mtanda cinali cotani?**
   Yankho: Kuyanjanitsa anthu ocimwa ndi Mulungu mwa kucotsa macimo ao kotero kuti iwo ali olungama pa maso a Mulungu (Yohane 1.29, 1 Yohane 4.10, Tito 2.14, 2 Akorinto 5.21).
7. **Ndime ya 4 imagwiritsidwa nchito kuonetsa kuti Mulungu afuna anthu ake kukhala athanzi masiku onse. Kodi tingayankhe bwanji iwo amene aphunzitsa tero?**
   Yankho: Colinga ca imfa yake pa mtanda cinali cakuti ayanjanitse ife ndi Mulungu (Aroma 5.10, 1 Petro 3.18). Ici citanthauza kuti aliyense wokhulupirira mwa Yesu amasulidwa ku temberero la macimo pompano. Baibulo sikamba kuti Akristu apulumutsidwa ku matenda pompano. Tibvutikabe ndi kudwalabe mpaka Yesu abwereranso kukonzekeranso ndithu zonse ngakhale matupi athu. Ganiziraniko citsanzo ca dzuwa. Dzuwa lisanaturuke tingaone kuunika kwake: ico ndico cizindikiro kuti mosacedwa dzuwa lidzaoneka. Ndi cimodzi-modzi m'Cikristu: mizimu yathu ndi yoomboledwa ku zotsatira zonse za macimo ndipo kuomboledwatu kwa matupi athu kudzacitika m'tsogolo (Aroma 8.18-23, Afilipi 3.21).

*Kuyankha mazunzo*

- Werengani pamodzi 2 Akorinto 12.8-10, 2 Akorinto 1.3 ndi 4 ndi Yakobo 5.13-15 ndipo yankhani mafunso awa.

8. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za kuyankha/kuthana ndi mazunzo?**

Yankho: Khalani olimba ndipo khazikikani m'cikhulupiriro (Yohane 16.33), kondwerani, pempherani ndi kumvetsetsa kuti kuzunzika m'njira yacikristu kuli ndi zipatso zabwino (cipiriro, cizolowezi ndi ciyembekezo, Aroma 5.3-5). Ciriconse cimene tiphunzira m'nsautso tiyenera kuuza anthu ena kuti iwo alimbikitsidwe (2 Akorinto 1.3 ndi 4). M'2 Akorinto 4.16-18 ndi 2 Akorinto 5.1 Mulungu atiphunzitsa kuti sitiyenera kutaya mtima: m'zocitika zobvuta Mulungu atikonzanso ku ulemerero wake.

9. **Werenganinso Yakobo 5.13-15. Kodi ndi ciani ceniceni cimene ciciritsa anthu odwala monga mwa ndime iyi?**
   Yankho: Cociritsa ndico pemphero pakuti mphamvu siili mwa ife koma mwa Mulungu. Mafuta achulidwa pakuti akhala mankhwala ololeka. Onani kuti si mankhwala amene aciritsa, koma Mulungu. Osaika ciyembekezo canu mwa mankhwala kapena miyambo koma mwa Mulungu (2 Mbiri 16.12). Zindikirani kuti kupemphera si kutanthauza kupangitsa Mulungu kucita zimene tifuna (tidzaphunzirako zina zambiri m'phunziro 5)
10. **Kodi muganiza ciani za anthu amene akhulupirira kuti yankho la mazunzu lipezeka mwa pemphero la mbusa, mneneri, bishop kapena munthu wina?**
    Yankho: M'Baibulo sitiwerenga za anenera okamba kuti, 'Bwerani kwa ine kuti Mulungu angakuthandizeni'. Iwo adziika m'kati osati Mulungu! Kuli kusiyana kwakukulu! Iwo ndiwo aneneri onama. Baibulo litilimbikitsa kupempherana. Mkristu aliyense ali ndi ciyandiko colimba cimodzimodzi monga Akristu anzake (Aefeso 3.12). Baibulo siipatsa mpata ya mkhalapakati wina aliyense koma Yesu yekha. Tidzaphunzirako zina zambiri m'phunziro 5.

*Kutha kwa mazunzo*

- Werengani pamodzi Cibvumbulutso 20.12-15 ndi Cibvumbulutso 21.1-4 ndipo yankhani mafunso awa.

11. **Werenganinso Cibvumbulutso 20.15. Matupi a iwo osalembedwa m'buku la moyo adzazunzika muyayaya. Kodi kutanthauza ciani kusalembedwa m'buku la moyo?**
    Yankho: Kutanthauza kukhala kopanda umoyo wauzimu. Aliyense amene sanalandire Yesu ndiye wakufa m'uzimu ngakhale munthuyo anadzipereka ku calichi kapena anacita zodabwitsa (Mateyu 7.22). Iwo okha amene anadzipereka kwa Yesu kupeza cipulumutso ndi nchito ya kuyanjana, iwo amene analandira umoyo wauzimu wocokera kwa Mulungu, iwo ndiwo olembedwa m'buku la moyo.
12. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za matupi a anthu a Mulungu?**
    Yankho: Mulungu adzawasamalira. Iye adzatha mazunzo ndi matenda ao. M'Afilipi 3.20 ndi 21 tiwerenga kuti matupi a anthu ake adzalingana ndi thupi la Yesu. Ici citanthauza kuti matupi ao adzakhala oyenerera.
13. **Kodi kutanthauzanji kuti zoyambazo zapita (Cibvumbulutso 21.4)?**
    Yankho: Kutanthauza kuti kumwamba ndi dziko lapansi zidzakonzedwanso. Zonse zidzakhala zatsopano. Pa dziko latsopano sikudzakhala kuzunza ndi kudwala. Sikudzakhala matenda kwa iwo amene analandira cikhululukiro ca macimo ao (Yesaya 33.24).
14. **Kodi mudzakhala kuti muyayaya?**
    Yankho: Lolani aliyense kuyankha pa yekha. Yesetsani kuwafulumizitsa kupeza cipulumutso mwa Yesu.

## 4. Kupumula (10 minutes)

- Ngati aphunzi afuna, aloleni kusewera sewero pa nthawi yopumula. Lolani mphunzi m'modzi kukhala patsogolo pa gulu ndi kuganizirako cinthu cimodzi (mwacitsanzo galu). Lolani aphunzi ena onse kufunsa mphunziyo mafunso kukafufuza cimene mphunziyo ali

kuganizirako koma mphunziyo aloledwa kuyankha cabe 'inde' kapena 'iai' pa mafunso ofunsidwa. Ndiye anthu ayenera kufunsa mafunso omwe angayankhidwe ndi 'inde' kapena 'iai' kukafufuza cimene mphunziyo ali kuganizirako.

## 5. Zolowapo (45 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono ndipo patsani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti akambireko.

**Colowapo 1 Misheck ndi Dainess**

Misheck ndi Dainess ali ndi ana atatu. Tsiku lina m'modzi wa ana ao adwala kwambiri. Misheck ndi Dainess sabvomerezana pa kucita ciani. Misheck afuna kuyembekeza masiku angapo kuona ngati mwana wao apola. Afuna kupatsa Mulungu mpata kucitapo kanthu. Dainess afuna iwo kupita ku cipatala kukapeza thandizo. Ambuya wa Dainess akamba kuti njira yofulumiza ndi yapafupi ndiyo kupereka mwana ku ng'anga amene akhala pafupi.

1. Kodi bvuto lingakhale lotani ngati Misheck ndi Dainess ayembekeza? Kodi bvuto lingakhale lotani ngati iwo alondola uphungu wa Dainess wa kupereka mwana ku cipatala? Kodi bvuto lingakhale lotani ngati iwo amvera ambuya wa Dainess amene anawauza kupereka mwana ku ng'anga?
2. Kodi mungalangize Misheck ndi Dainess kucita ciani?

**Colowapo 2 Patricia**

Patricia ndiye mai wosakwatiwa amene ali ndi ana awiri. Analapa macimo ake ndipo akhulupirira Yesu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye wake. Tsiku lina Patricia adwala kwambiri. Anthu aopa kuti Patricia angamwalire. Patricia sanayembekeze kuti angadwale kwambiri. Aganiza, 'Baibulo likamba kuti zinthu zonse zithandizana kucitira ubwino iwo amene akonda Mulungu (Aroma 8.28). Ndikonda Mulungu. Ncifukwa ciani ndadwala?'

1. Kodi mudziwa anthu amene akhulupirira kuti Akristu sayenera kudwala?
2. Kodi munganene ciani kwa Patricia? Ngati muli ndi Baibulo, werengani Aroma 8.28 ndi 29 ndipo fotokozani ndime izi.

**Colowapo 3 Oscar**

Oscar anayamba kusamvera bwino caka catha. Ku cipatala anapeza kuti ali ndi bvuto la ku mtima kwake. Anapatsidwa mankhwala. Koma bvuto lake linapitirira. Oscar anapita ku mneneri kugula mafuta odalitsika (anointed oil). Oscar anagwiritsa nchito mafuta odalitsika koma saona kusiyana kalikonse. Oscar adabwa kuti bvuto lingakhale ciani.

1. Kodi mudziwa anthu amene amagwiritsa nchito mafuta odalitsika napola?
2. Kodi mudziwa anthu ogwiritsa nchito mafuta odalitsika koma sanapole?
3. Kodi nciani cimene cipangitsa mafuta kukhala odalitsika? Kodi mafuta odalitsika opezeka kuti?
4. Kodi muganiza kuti cifukwa nciani Oscar sanapole iye angakhale kugwiritsa nchito mafuta odalitsika?
5. Kodi mungalangize Oscar kucita ciani?

**Colowapo 4 Marita**

Marita ndi mai wokalamba. Ali ndi nthenda ya khansa. Tsiku lirilonse thupi lake limawawa. Koma sadandaula kwambiri. Pamene ana ao awafunsa kuti akumva bwanji Marita ayankha, 'Ndikomana ndi kuwawa. Tsiku lirilonse pamene ndauka sindidziwa kuti ndidzakwaniritsa bwanji kukhala moyo tsiku limenelo. Koma ndidziwa kuti Mulungu andisamalira. Anandipulumutsa ku macimo anga ndipo andipatsa mphamvu. Si cinthu ca pafupi kukhala ndi

nthenda ya khansa. Nthawi zambiri ndinapempha Mulungu kundiciritsa koma sanacite tero mpaka tsopano. Ngati ici ndi cabwino coposa, ndifuna kubvomereza ndi kumyamikira Mulungu. Kufuna kwake kucitike m'umoyo wanga'.

1. Kodi kutanthauza ciani kuti kufuna kwa Mulungu kucitike?
2. Lingalirani umoyo wanu. Kodi mumayankha bwanji matenda ndi zobvuta zina?

**Colowapo 5 Christoffer**

Caka catha pamene Christoffer anayenda ku Lusaka, iye anapezeka m'ngozi. Basi imene inanyamula Christoffer inagundana ndi basi ina. Ena onyamulidwa paulendo anafa. Ambiri anapweteka. Christoffer anapwetekanso. Anasungidwa m'cipatala kwa masabata anai. Anthu a ku mudzi wa Christoffer anayamba kusinkhasinkha zifukwa za ngozi.

1. Kodi zifukwa za mabvuto zoperekedwa ndi anthu ndizo zotani?
2. Kodi Baibulo likamba ciani za zifukwa za mabvuto?
3. Kodi tiyenera kuyankha bwanji pamene tikomana ndi mabvuto?

- Itakomana 10 minutes kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco.

**Misheck ndi Dainess**

1. **Kodi bvuto lingakhale lotani ngati Misheck ndi Dainess ayembekeza? Kodi bvuto lingakhale lotani ngati iwo alondola uphungu wa Dainess wa kupereka mwana ku cipatala? Kodi bvuto lingakhale lotani ngati iwo amvera ambuya wa Dainess amene anawauza kupereka mwana ku ng'anga?**

   Yankho: Ngati ayembekeza, alephera kulondola njira zimene Mulungu anatipatsa. Iwo akapereka mwana wao ku cipatala, angaiwale kuti afunika thandizo ndi dalitso la Mulungu la pa kuchiza. Iwo akapita ku ng'anga adzacitira mwano Mulungu amene satilola kupempha ng'anga thandizo lake (Deuteronomo 18.10-13, Levitiko 19.31, Yesaya 8.19)

1. **Kodi mungalangize Misheck ndi Dainess kucita ciani?**

   Yankho: Ayenera kupempha Mulungu thandizo ndi nzeru ndipo ayeneranso kupita ku cipatala popempha Mulungu kudalitsa mankhwala.

**Patricia**

1. **Kodi mudziwa anthu amene akhulupirira kuti Akristu sayenera kudwala?**

   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi munganene ciani kwa Patricia? Ngati muli ndi Baibulo, werengani Aroma 8.28 ndi 29 ndipo fotokozani ndime izi.**

   Yankho: Akristu angadwale. Cifukwa ca Aroma 8.28 tingaganize kuti Mulungu afuna anthu ake kukhala ndi thanzi nthawi zonse osati kudwala konse, pakuti kukhala ndi moyo ndi kwabwino. Koma ngati tiwerenga Aroma 8.29 tiphunzira kuti Mulungu akamba za ubwino wa kukhala monga Yesu. M'zocitika zonse Mulungu apangitsa anthu ake kusanduka kukhala monga Yesu

**Oscar**

1. **Kodi mudziwa anthu amene amagwiritsa nchito mafuta odalitsika napola?**

   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mudziwa anthu ogwiritsa nchito mafuta odalitsika koma sanapole?**

   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.

3. **Kodi nciani cimene cipangitsa mafuta kukhala odalitsika? Kodi mafuta odalitsika opezeka kuti?**
   Yankho: Aloleni kupereka mayankho.
   M'Cipangano Cakale tiwerenga za zinthu zosakaniza popanga mafuta odalitsika ogwiritsidwa nchito kuika cizindikiro pa Kacisi ndi zimene zinakhalamo zopatulika za Mulungu (Eksodo 30.23-24). Baibulo siikamba kuti m'mafuta odalitsika muli mphamvu yauzimu. Mulungu sanalole munthu wina aliyense kupanganso mafuta odalitsika (Eksodo 30.32-33).
   M'Cipangano Catsopano tiwerenganso za mafuta (Mateyu 6.17, Marko 6.13, Yakobo 5.14) koma Baibulo siikamba kuti mafutawa ndi odalitsika. M'Cipangano Catsopano Baibulo likamba za mafuta a masiku onse. M'Cipangano Catsopano sitiwerenga mau olimbikitsa kugwiritsa nchito mafuta odalitsika komanso sitiwerenga kuti Mulungu atiletsa kusewenzetsa mafuta odalitsika.
   Masiku ano anthu ambiri akhulupirira kuti muli mphamvu mu mafuta odalitsika ocokera kwa anthu opatulika a Mulungu. Tifunika kucenjera:
   - Kodi ndi mphamvu yotani ndi yocokera kwa yani?
   - M'phunziro 5 tidzaphunzira kuti aneneri alibe mphamvu yapadera. Akristu aliyense aloledwa kubwera pafupi ndi Mulungu mokhazikika mtima ndi moyandikira kwaufulu.
   - Nthawi zambiri m'mitima yao anthu adalira pa mafuta osati pa Mulungu.
4. **Kodi muganiza kuti cifukwa nciani Oscar sanapole iye angakhale kugwiritsa nchito mafuta odalitsika?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao. Ayenera kumvetsa kuti kulibe mphamvu mwa mafuta odalitsika koma mwa Yesu. M'zonse zimene ticita ndi kugwiritsa nchito, cinthu cingatithandiza cabe ngati Mulungu afuna kuti citithandiza.
5. **Kodi mungalangize Oscar kucita ciani?**
   Yankho: Osadalira pa mafuta, koma pa Mulungu. Oscar ayenera kuphunzira kunena, 'Kufuna kwanu kucitidwe'.

**Marita**

1. **Kodi kutanthauza ciani kuti kufuna kwa Mulungu kucitike?**
   Yankho: Kutanthauza kukhulupirira kuti kufuna kwa Mulungu ndi kwabwino, kuti Iye alamulira ndipo kutanthauzanso kudzipereka kwa Iye m'cocitika ciriconse. Ngati Iye aticiritsa tibvomera kufuna kwake. Ngati saticiritsa tibvomerezanso kufuna kwake. Phunziro iri ndi lalikulu. Osaganiza kuti kukanira moonadi zofunafuna zathu ndi kubvomereza kufuna kwa Mulungu ndiko cinthu capafupi. Tikhoza kucita tero mwa cisomo mwa Yesu cabe. M'2 Akorinto 4.16-18 ndi 2 Akorinto 5.1 tiwerenga kuti tingakhale tadwala tikhale ndi ciyembekezo.
2. **Lingalirani umoyo wanu. Kodi mumayankha bwanji matenda ndi zobvuta zina?**
   Yankho: Aloleni aliyense kuyankha pa yekha.

**Christoffer**

1. **Kodi zifukwa za mabvuto zoperekedwa ndi anthu ndizo zotani?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao.
2. **Kodi Baibulo likamba ciani za zifukwa za mabvuto?**
   Yankho: Baibulo likamba kuti ciyambi ca mabvuto onse ndico chimo loyamba la Adamu ndi Hava m'Paradaiso. Atacimwa mabvuto ena onse anayamba. Pamene tiwerenga Baibulo tingapeze zifukwa zina za kukomana ndi mabvuto, mwacitsanzo chimo la

munthu mwini, Satana, makhalidwe ao kapena Mulungu amene agwiritsa nchito bvutolo ndi colinga (onani Kuwerenga Baibulo, funso loyamba).

3. **Kodi tiyenera kuyankha bwanji pamene tikomana ndi mabvuto?**
   Yankho: Nthawi zonse tiyenera kuyang'anira Mulungu. Gwiritsani nchito njira zololedwa ndi Mulungu. Lolani Mulungu kucita zabwino zoposa.

## 6. Finish (5 minutes)

- Fupikitsani zimene zaphunzitsidwa lero: Kuzunzika ndi kudwala ndiko mbali ya kukhala ndi moyo. Kulibe kupatula kwa Akristu. Tiyenera kudzipereka kwa Mulungu ndi kupitiriza kukhala olimba m'cikhulupiriro ndiponso kukhulupirira Mulungu pa nzeru zake kutisunga, kutithandiza ndi kutiphunzitsa mwa Mzimu wake Woyera. Tiloledwa kugwiritsa nchito mankhwala ololeka ndipo tidalira pa Mulungu kuticiritsa. Tipempha Mulungu kucita zotipindulitsa ndiponso zimene ziri zabwino kwa ulemerero wake.
- Pempherani.

## Phunziro 3 Cuma ndi umphawi

<u>Zofunikira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 2: Kuzunzika ndi kudwala ndiko mbali ya kukhala ndi moyo. Kulibe kupatula kwa Akristu. Tiyenera kudzipereka kwa Mulungu ndi kupitiriza kukhala olimba m'cikhulupiriro ndiponso kukhulupirira Mulungu pa nzeru zake kutisunga, kutithandiza ndi kutiphunzitsa mwa Mzimu wake Woyera. Tiloledwa kugwiritsa nchito mankhwala ololeka ndipo tidalira pa Mulungu kuticiritsa. Tipempha Mulungu kucita zotipindulitsa ndiponso zimene ziri zabwino kwa ulemerero wake.

## 2. Sewero (10 minutes)
*Mayankho a ziganizo adzapatsidwa pa kuwerenga Baibulo. Cifukwa cace osatenga nthawi yaitali pa mbali iyi.*

- Werengerani aphunzi ziganizo izi. Ngati abvomera ayenera kukweza manja ao. Ngati sabvomera sayenera kukweza manja ao. Aloleni kufotokozera mayankho ao.
  a. Anthu osauka athandiza bwino kwambiri anthu ena kuposa anthu acuma.
  b. Ndalama ikhoza kuthetsa bvuto lina lirilonse.
  c. Umphawi ndiwo temberero.
  d. Kulibe kusiyana pakati pa Akristu ndi iwo amene sali Akristu m'njira imene agwiritsa nchito ndalama yao.
  e. Kukhulupirira Mulungu ndi capafupi ngati tasauka.
  f. Anthu a Mulungu afunika kulemera.

## 3. Cuma ndi umphawi m'Baibulo – Kuwerenga Baibulo (90 minutes)
*Zonse ndi za Mulungu*
- Werengani pamodzi <u>Yeremiya 27.5</u> ndi <u>1 Samueli 2.7</u> ndipo yankhani mafunso awa.
  1. **Mulungu ndiye Wolenga ndi Mwini wa zonse. Kodi citanthauza ciani kuti ife ndife akapitao ake?**
     Yankho: Citanthauza kuti tiyenera kusamalira zonse zimene Iye atipatsa. Tiyenera kumfotokozera njira yamene tagwiritsa nchito zonse, ngati tiri ndi zambiri komanso ngati tiri ndi zocepa (Genesis 2.15). Tiyenera kugwiritsa nchito ciriconse cimene tiri naco m'njira imene Mulungu afuna: molungama, mokonda cifundo ndi moyenda modzicepetsa ndi Mulungu (Mika 6.8).
  2. **Kodi mungayankhe bwanji anthu amene anena kuti umphawi ndiwo temberero locokera kwa Satana?**
     Yankho: Mulungu ndiye Mwini wa zonse ndipo amapereka m'njira imene afuna. Acuma ndi aumphawi ndiwo ofunikira pa maso pa Mulungu. Satana akhoza kucita cabe zimene Mulungu amlola kucita (onani citsanzo ca Yobu m'mene Satana anayenera kupempha cilolezo ca Mulungu). Satana safanana ndi Mulungu mphamvu: Mulungu ndiye Wamphamvuyonse.

*Kugwiritsa nchito katundu wathu*

- Werengani padmodzi <u>Deuteronomo 15.7</u> ndi <u>Macitidwe 20.35</u> ndipo yankhani mafunso awa.

3. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za kuyankha pamene Mulungu atipatsa cinthu?**
   Yankho: Khalani oyamikira, osadzikweza. Ngakhale tagwira nchito molimba, ndi Mulungu amene anatipatsa mphamvu kugwira nchito. Kondwerani ndi zimene Mulungu apatsa (Mlaliki 5.18 ndi 19). Khalani opereka mwaulere. Osagwiritsa nchito modzikonda anthu osauka ndi opanda mphamvu (Yakobo 5.1-6)
4. **Kodi Macitidwe 20.35 itiphunzitsa ciani za njira ya kupeza cuma?**
   Yankho: Tiyenera kugwira nchito kuti tikhoza kugawira za zimene tiri nazo (Aefeso 4.28). Mulungu amadalitsa anthu mwa nchito yao.

*Cuma monga coleperetsa*

- Werengani pamodzi <u>Marko 10.24-27</u> ndi <u>1 Timoteo 6.5-10</u> ndipo yankhani mafunso awa.

5. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za cofunikira ca kukhala olemera?**
   Yankho: Si cofunikira konse. Komabe Baibulo liticenjeza kuti cuma cingatileperetse m'uzimu. Baibulo litilimbikitsa kuganizira zambiri za Kumwamba ndi kukhala okonzeka kupitako.
6. **Kodi cuma cingatileperetse m'njira yotani?**
   Yankho: Coopsa ndi cakuti tingaganizireko kwambiri zinthu zooneka ndi maso ndi za pansi m'malo mwa kuganizirako kwambiri zinthu zamuyaya ndi za Kumwamba. Cuma cingatisokoneze kuti tiiwale Mulungu ndi moyo m'mene Mulungu afuna ife kukhalira (Mateyu 6.24). Kudera nkhawa kwambiri zinthu za cuma ndi umoyo wa masiku onse kutionetsa kuti mitima yathu si yoyanjanitsidwa ndi Mulungu ndiponso kuti sitiri okonzeka kupita Kumwamba. Ganizirani citsanzo ca Mose amene anadziwa kuti kukhala ndi Mulungu mu umphawi ndi kwabwino kuposa kulemera kopanda Mulungu (Ahebri 11.24-26). Funsani aphunzi ngati ali okonzeka kusiya cuma ngati ciwapangitsa kucimwa (mwacitsanzo kuleka kuba, kuleka kukumba miyala mosagwirizana ndi malamulo, kuleka ufiti, kuleka kunama za ndalama).

- Werengani pamodzi <u>2 Akorinto 11.23-27, Ahebri 13.5</u> ndi <u>1 Timoteo 6.8</u> ndipo yankhani mafunso awa.

7. **Kodi mungayankhe ciani iwo amene anena kuti Mulungu afuna Mkristu aliyense kukhala wolemera?**
   Yankho: Si zoona. M'Baibulo tiwerenga zitsanzo zambiri za okhulupirira oona amene anali osauka (mwacitsanzo Marko 12.42, 1 Mafumu 17.12). Baibulo siika mlandu pa iwo pa kukhala osauka. Baibulo lilonjeza za kuyesetsa cuma.
8. **Kodi Mulungu atilola kulakalaka zocuruka nthawi zonse?**
   Yankho: Mulungu afuna kuti tikhala okwaniritsidwa ndi zimene tiri nazo. Ngati tisowa cinthu, tiloledwadi kumfunsa koma osakhala a umbombo. Baibulo litilimbikitsa kusalakalaka cuma ndi umphawinso (Miyambi 30.8 ndi 9).
9. **Kodi njira yeniyeni ya kukhala okwaniritsidwa ndi zimene tiri nazo ndiyo ciani?**
   Yankho: Tikhoza kukhala okwaniritsidwa moonadi ngati tidziwa kuti Mulungu ndi Mulungu wathu. Ngati tayanjanitsidwa naye mwa Yesu. Ngati Iye ndi Mulungu wathu, Iye atisamalira, adziwa zosowa zathu, aticitira zabwino koposa ndipo timkhulupirira kuti sadzatisiya konse (Ahebri 13.5). Ici sicitanthauza kuti nthawi zonse tidzakhala ndi zoculuka (onani yankho pa funso 7).

*Cuma ceniceni*

- Werengani pamodzi Luka 16.19-26 ndi Cibvumbulutso 3.17 ndi 18 ndipo yankhani mafunso awa:

**10. Kodi munthu mwini cuma anali wosauka m'njira yanji?**
Yankho: Anali wosauka pakuti sanali wokonzeka kukufmana ndi Mulungu. Anaganizira kwambiri cuma cosakhalitsa cooneka ndi maso m'malo mwa cuma camuyayaya cimene citanthauza kuyanjanitsidwa ndi Mulungu.

**11. Kodi kulemera koona kutanthauza ciani monga mwa ndime izi?**
Yankho: Kutanthauza kubwerezedwa m'ciyanjano cabwino ca Mulungu mwa Yesu Mpulumutsi. Mwa Yesu yekha macimo athu akhoza kukhululukidwa kotero kuti tibwerezedwe kwa Mulungu. Cifukwa ca Yesu yekha anthu adzaloledwa kukhala ndi Mulungu Kumwamba muyayaya kumene iwo sadzasowa konse cinthu ciriconse.

**12. Werenganinso Cibvumbulutso 3.17 ndi 18. Kodi kusauka m'mzimu kutanthauza ciani?**
Yankho: Kutanthauza kulekanitsidwa ndi Mulungu. Kukhala kopanda ciyembekezo ca umoyo wosatha. Kukhala yekha, wocimwa ndi pansi pa mkwiyo wa Mulungu cifukwa ca macimo. Kukhala kopanda umoyo wauzimu. Izi ndi m'mene ziliri kwa anthu amene sayanjanitsidwa ndi Mulungu. Tingakhale ndi ndalama zambiri koma ngati tikhala kopanda Yesu monga Mbuye ndi Mpulumutsi wathu, ndife osauka.

*Mulungu ndi wolemera m'uzimu, ife anthu ndife osauka m'uzimu*

- Werengani pamodzi Yesaya 55.1 ndi Aefeso 2.4-7 ndipo yankhani mafunso awa:

**13. Tawerenga kuti Mulungu ali wolemera cifundo (Aefeso 2.4). Kodi ici citanthauza ciani?**
Yankho: Citanthauza kuti Mulungu sasowa cifundo ndi cisomo ca kwa munthu wina aliyense amene abwera kwa Iye kukapeza cipulumutso. Mulungu afuna ndipo akhoza kupulumutsa wina aliyense. Mwa cifundo ndi cisomo asunganso anthu ake m'zocitika zonse (m'kulemera komanso m'kusauka) ndipo awabweretsa kwao Kumwamba.

**14. Kodi ndi m'njira yanji m'mene tikhoza kudziwa cifundo ca Mulungu pa ife tokha?**
Yankho: Mwa Yesu Mpulumutsi ndi Mkhalapakati. Cipulumutso ndico mphatso (Yesaya 55.1) imene Mulungu apatsa mwa cifundo ndi cisomo. Mphatsoyo ndi yoyenera kuposa cinthu ciriconse ca pa dziko lapansi. Kukhala woyanjanitsidwa ndi Mwini wa mlengamlenga! Mbuye wa makamu kukhala Tate wathu amene atisamalira! Kuloledwa kukhala naye muyayaya! Iwo amene alandira mphatso iyi yapadera aitanidwa kulemekeza Mulungu m'cocitika ciriconse ngati kuli umphawi komanso ngati kuli cuma (1 Akorinto 6.20).

- Tsirizani pa kunena kuti Mulungu akhozadi kutidalitsa ndi zinthu zooneka ndi maso koma sitiloledwa kukhala odziganizira mwa kuganizira kwambiri cuma.

## 4. Kupumula (10 minutes)

- Ngati aphunzi afuna, aloleni kusewera sewero pa nthawi ya kupumula. Funsani mphunzi m'modzi kukhala patsogolo pa gulu. Aloleni aphunzi ena kumfunsa mafunso. Mphunzi wokhala patsogolo saloledwa kunena mau 'iai' pa kuyankha. Ngati akamba 'iai' mphunziwo ayenera kukhala pansi ndipo mphunzi wina ayenera kupatsidwa mpata kukhala patsogolo ndi kuyankha mafunso.

## 5. Zolowapo (45 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono ndipo patsani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti akambireko.

**Colowapo 1 George**
George amalima molimbika koma saona zipatso za nchito yake. Usiku wina atumira foni mneneri amene alalikira pa wailesi. Mneneri auza George kuti aona ciwanda coletsa kutukuka. Mneneri auza George kumyendera kuti aononge mphamvu ya ciwanda. Mneneri anena kuti Mulungu afuna George kukhala wolemera nthawi zonse.

1. Kodi munamva anthu onena kuti Mulungu afuna ake kulemera nthawi zonse?
2. Kodi mungauze ciani George kuti athandizike?

**Colowapo 2 Davison ndi Patricia**
Davison ndi Patricia ali m'ukwati. Ali ndi ana asanu ndi m'modzi. Davison amagwira nchito molimbika kuti apatse banja lake zonse zimene iwo asowa. Davison ndi mkazi wake akonda kuthandiza anthu ena obvutika. Iwo omwe alibe zambiri koma athandizanso anthu ena. Anena, 'Mulungu ndi wacifundo kotero kuti anatipatsa Mwana wake Yesu kukhala Mphatso wamkulu koposa kuti tayanjanitsidwa naye. Mulungu ndi wacifundo ndipo amatithandiza tsiku lirilonse. Cifukwa cace tifuna kuthandiza iwo amene asowa zimene ife tiri nazo'.

1. Kodi mudziwa anthu amene akonda kupatsa anthu ena?
2. Kodi tingathandize anthu ena m'njira zotani?

**Colowapo 3 Albert ndi Anna**
Albert ndi Anna ali ndi mwana m'modzi. Albert amagwira ganyu ndipo akwaniritsa kupeza ndalama zokwanira banja lake. Anna sakhutitsidwa ndi ndalama zimene Albert apeza. Anna apeza nchito ku malo odyera kumene aphika cakudya masiku onse. Cifukwa ca ndalama yopezedwa ndi Anna, iwo akwaniritsa kutuma mwana wao ku private school. Koma patapita nthawi Albert ayamba kudandaula kuti mkazi wake alephera kucita nchito kunyumba zimene iye ayenera kucita.

1. Kuganizira kwambiri za cuma kungayambitse mabvuto ndi kungatilepheretse. Fotokozani m'mene izi zinacitika m'nkhani iyi.
2. Kodi mungapangire Albert ndi Anna kucita ciani?

**Colowapo 4 Lovemore ndi Vestina**
Lovemore ndi Vestina analowa m'ukwati caka catha. Nthawi zambiri iwo asowa cakudya ndi zobvala kunyumba. Vestina alimbikitsa Lovemore kucita cinthu kuti athandizike koma Lovemore ayankha, 'Ngati ndiyamba kukapeza ndalama, citanthauza kuti si ndife okhutiritsidwa ndi zimene tiri nazo ndipo ico ndi chimo. Komanso Baibulo likamba kuti, 'Odala ali osauka' ndiye pa maso pa Mulungu kusauka ndi kwabwino kuposa kulemera'. Vestina sakondwera konse koma Lovemore safuna kusintha maganizo ake. Ngati iwo alibe cakudya, Vestina apita kukabera anthu okhala pafupi nao.

1. Kodi mudziwa anthu amene akhulupirira kuti osauka ndiwo okhulupirira abwino kuposa anthu acuma?
2. Kodi mungauze ciani Lovemore ndi Vestina?

**Colowapo 5 Benson ndi Dalitso**
Benson ndiye membala ku calichi yanu. Mnzake Dalitso samapita ku calichi. Nthawi zambiri Dalitso ayesa kuzindikiritsa Benson kuti aleke kupita ku calichi. Anena, 'Kulibe Mulungu. Mungoononga nthawi. M'malo mwa kupita ku calichi pa Sondo muyenera kulima kuti

mukhale ndi cimanga cambiri monga ine. Mungalemere ngati muleka kupita ku calichi ndiponso ngati mugwira nchito kwambiri.'

1. Kodi mudziwa anthu amene sakhulupirira kuti Mulungu aliko?
2. Kodi mungapangire Benson kuti ayankhe bwanji Dalitso?

**Colowapo 6 Kondwerani ndi Mercy**
Kondwerani ndi Mercy ali m'ukwati zaka zitatu. Iwo abvutika kukhala ndi moyo. Mercy anena, 'Abusa wathu sali bwino. Afuna cabe ndalama zathu. Iye alemera cifukwa ca copereka. Ife tasauka cifukwa timpatsa ndalama zathu. Tifunika kupita ku calichi ina'.

1. Kodi mudziwa anthu amene alimbana za kupereka copereka?
2. Kodi mungapangire Kondwerani ndi Mercy kucita ciani?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali tero:

**George**

1. **Kodi munamva anthu onena kuti Mulungu afuna ake kulemera nthawi zonse?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mungauze ciani George kuti athandizike?**
   Yankho: Kulibe bvuto kupempha atsogoleri anzeru ndi a za m'Baibulo thandizo ndi uphungu. Khalani maso pa kufunsa yani. George ayenera kumvetsa kuti cuma ndi umphawi zonse ziwiri ziri pansi pa ulamuliro wa Mulungu (1 Samueli 2.7). Si zoona kuti Mkristu aliyense afunika kulemera (onani za m'Kuwerenga Baibulo m'mene taphunzira kuti m'Baibulo munali okhulupirira oona ambiri amene sanalemere ndiponso kuti Mulungu aticenjeza kuti cuma cingatilepheretse).

**Davison and Patricia**

1. **Kodi mudziwa anthu amene akonda kupatsa anthu ena?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi tingathandize anthu ena m'njira zotani?**
   Yankho: Aloleni kupereka zitsanzo. Mwacitsanzo: kupereka ndalama ku calichi kuti a ku calichi angathandize paliponse popezeka bvuto, kugawana kukolola, kupatsa cakudya, kulankhula nao kuwalimbikitsa ndi kuwathandiza kupeza njira zodzisamalira.

**Albert and Anna**

1. **Kuganizira kwambiri za cuma kungayambitse mabvuto ndi kungalepheretse. Fotokozani m'mene izi zinacitika m'nkhani iyi.**
   - Anna anagwira nchito masiku onse kutanthauza kuti sanakhoze kupita ku calichi. Kodi angalimbike bwanji m'uzimu ngati aganiza cabe za zofunikira za thupi osati za zofunikira za uzimu?
   - Mwamuna wake anayamba kudandaula kuti Anna analephera kucita nchito ya pa nyumba. Iwo anali ndi ndalama koma analibe mtendere. Aloleni aphunzi kukambirana kuti cofunikira koposa ndico ciani.
2. **Kodi mungapangire Albert ndi Anna kucita ciani?**
   Anna ayenera kumvetsa kuti ndalama si yofunikira koposa. Cofunikira koposa ndi kudziwa Mulungu mwa Yesu Kristu Mpulumutsi ndi kukhala monga mwa cifuniro cace. Ngati cuma citileperetsa kukhala ndi umoyo woopa Mulungu, cabwino koposa ndico kusakhala ndi ndalama koma kutumikira Mulungu. Ndithu ndi cofunikira kwambiri kuti banja likhale ndi moyo, koma pa nkhani ya Albert ndi Anna iwo anakhoza kukhala ndi moyo koma kulakalaka zocuruka kwa Anna kunapangitsa mabvuto.

**Lovemore and Vestina**

1. **Kodi mudziwa anthu amene akhulupirira kuti osauka ndiwo okhulupirira abwino kuposa anthu acuma?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mungauze ciani Lovemore ndi Vestina?**
   Yankho: Mulungu afuna kuti tigwire nchito molimbika kuthandiza mabanja athu ndi anthu obvutika (2 Atesalonika 3.12, Aefeso 4.28). Si zoona kuti anthu onse osauka apezeka m'banja la Mulungu mopanda bvuto. Anthu onse, acuma ndi osauka onse awiri, afunika kuyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa Yesu Kristu. Baibulo siikamba kuti 'Odala osauka' koma 'Odala osauka mumzimu' (Mateyu 5.3). Ici citanthauza iwo amene amvetsa kuti alibe kalikonse mwa iwo okha kamene kangawapangitse kukhala olandiridwa ndi Mulungu, koma amvetsa kuti asowa zonse ndipo adalira pa Yesu yekha.

**Benson ndi Dalitso**

1. **Kodi mudziwa anthu amene sakhulupirira kuti Mulungu aliko?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mungapangire Benson kuti ayankhe bwanji Dalitso?**
   Yankho: Benson angayese kulankhula ndi Dalitso. Angafotokozere kuti ncifukwa ciani iye akhala wotsimikiza kuti Mulungu aliko. Zonse zimene tiri nazo ndizo mphatso: sitikhala ndi cinthu ciriconse ca ife mwini. Ngakhale timalima kwambiri, wotipatsa mphamvu kucita tero ndi Mulungu. Benson ayenera kumpempha Mulungu nzeru ndi thandizo kukamba mau akucirikiza pa nthawi yabwino.

**Kondwerani and Mercy**

1. **Kodi mudziwa anthu amene alimbana za kupereka copereka?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mungapangire Kondwerani ndi Mercy kucita ciani?**
   Yankho: Ayenera kufufuza ngati mbusa wao ndi mbusa woona monga mwa Baibulo. Azibusa ena angolalikira kuti akhale ndi ndalama. Mwina mbusa wao ndi mbusa wonama. Ngati ziri tero, ayenera kupeza calichi ina kumene Uthenga Wabwino alalikidwa. Ayenera kufufuza (phunziro 5). Ayenera kumvetsa kuti Mulungu ndi Mwini wa zonse. Cifukwa cace kupereka copereka ndi kwabwino.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fupikitsani zimene zaphunzitsidwa lero: Mulungu ndiye Mwini zonse. Tiyenera kugwiritsa nchito ciriconse cimene tiri naco ku ulemerero wake ndi kukhala monga mwa cifuniro cace. Baibulo likamba za Akristu olemera monga likambanso za Akristu osauka. Cuma cingatilepheretse m'uzimu. Mphatso yaikulu koposa ndiyo Yesu Mpulumutsi. Funani kupeza Iye, osati cuma poyamba.
- Pempherani.

**Phunziro 4 Mdima ndi Kuunika**

<u>Zofunikira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 3: Mulungu ndiye Mwini zonse. Tiyenera kugwiritsa nchito ciriconse cimene tiri naco ku ulemerero wake ndi kukhala monga mwa cifuniro cace. Baibulo likamba za Akristu olemera monga likambanso za Akristu osauka. Cuma cingatilepheretse m'uzimu. Mphatso yaikulu koposa ndiyo Yesu Mpulumutsi. Funani kupeza Iye, osati cuma poyamba.

## 2. Mdima motsutsana ndi Kuunika (10 minutes)
- Akumbutseni mwacidule zimene zinacitika pamene Adamu ndi Hava anacimwa. Mwa kusamvera Mulungu, iwo anadziika okha pansi pa ulamuliro wa Satana (kapena mdyerekezi) mwakufuna kwao. Kuyambira pamenepo, aliyense ali pansi pa ulamuliro wa Satana mwacibadwa (Aefeso 2.2-3). Ici citanthauza kuti *aliyense* ali pansi pa ulamuliro wa Satana (pokhapokha titapulumutsidwa mwa cisomo monga momwe tidzaphunzirira mtsogolo lero) osati okhawo omwe adzipereka kwa Satana mwanjira inayake yapadera.
- Lembani mzere pa bolodi kuyambira pamwamba mpaka pansi. Mbali imodzi iyimirira Mulungu ndi Ufumu wake, mbali inayo iyimira Satana ndi ufumu wake.
- Werengani mau awa limodzi ndi limodzi ndipo funsani aphunzi kuti ndi ufumu uti umene mauwo ayenera bwino. Lembani mayankho ao pa bolodi. <u>Musakambirane pa mayankho cifukwa mayankho adzaperekedwa m'phunziro la Baibulo.</u>
  *Kuunika, mdima, cikondi, ucimo, kukhulupirika, mantha, kukayika, moyo, mtendere, msokonezo, udani, cimwemwe, cionongeko, cifundo, mabodza, coonadi, wamphamvuyonse, woyera, cinyengo, malire.*
  Mayankho:

| Mulungu ndi Ufumu wake | Satana ndi ufumu wake |
|---|---|
| Kuunika | Mdima |
| Cikondi | Ucimo |
| Kukhulupirika | Mantha |
| Moyo | Kukayika |
| Mtendere | Msokonezo |
| Cimwemwe | Udani |
| Cifundo | Cionongeko |
| Coonadi | Mabodza |
| Wamphamvuyonse | Cinyengo |
| Woyera | Malire |

## 3. Kuwerenga Baibulo (120 minutes)

*A. Kodi Satana ndani?*

- Werengani pamodzi Yuda 1.6, Cibvumbulutso 12.7-9 ndi Yobu 2.6 ndipo yankhani mafunso awa:

1. **Kodi Satana ndani?**
   Yankho: Satana ndi mngelo amene anacimwira Mulungu ndipo anapitikitsidwa kumwamba.
2. **Kodi angelo a Satana ndani?**
   Yankho: ziwanda
3. **Kodi colinga cacikulu ca Satana ndi ciani?**
   Yankho: kunyengerera anthu.
4. **Kodi Yobu 2.6 itiphunzitsa ciani pa mphamvu ya Satana?**
   Yankho: mphamvu ya Satana ili ndi malire. Sangacite ciriconse pokhapokha Mulungu amulola kutero.

(kwa aphunzitsi: tiwerenga zina za Mikayeli mkulu wa angelo mu Yuda 1.9, Danieli 12.1, Danieli 10.13 ndi 21).

- Werengani pamodzi Yohane 8.44 ndi 1 Petro 5.8-9 ndipo yankhani mafunso awa:.

5. **Cifukwa ndi ciani Satana ndi wochedwa wambanda ndi wabodza kuyambira paciyambi?**
   Yankho: ananamiza Hava ndipo anatsogolera anthu onse ku ciononongeko (imfa yakuthupi ndi yauzimu).
6. **Cifukwa nciani Satana ndi wochedwa mdani wathu (1 Petro 5.8-9)?**
   Yankho: cifukwa cakuti amayesa, amanyenga, amaneneza ndipo safuna kuti anthu akhala mogwirizana ndi Mulungu ndi anthu ena.
7. **Fotokozani cifukwa cake Satana ayerekezeredwa ndi mkango wobuma (1 Petro 5.8-9).**
   Yankho: pakuti afuna kuononga anthu.
8. **Kodi citanthauzanji kuti Satana adzionetsa ngati mngelo wa kuunika (2 Akorinto 11.14)?**
   Yankho: Satana amayesa kuoneka ngati mthenga wa Mulungu. Nthawi zambiri zinthu zoipa zioneka zabwino m'malo mooneka zonyansa kapena zoopsa. Satana amagwiritsa nchito cinyenjo kuti apangitse bodza kuoneka ngati coonadi. Atumwi onyenga amacita cimodzimodzi: anena kuti akamba m'malo mwa Mulungu koma amasoceretsa anthu kutali ndi coonadi ndi cilungamo.

*B. Kodi Mulungu anena ciani za kugwirizana ndi Satana ndi zocita zake?*

- Werengani pamodzi Deuteronomo 18.9-14, Yesaya 8.19 ndi 1 Akorinto 10.20-21 ndipo yankhani mafunso awa:

9. **Kodi Mulungu atiphunzitsa ciani m'ndime izi pa nkhani yopita kwa ng'anga kapena kwa African doctor amene amalosera?**
   Yankho: izi ndi zonyansa pamaso pa Ambuye. Satilola kucita tero. Ngati tilosera maula, ndife oipa ndi onyansa pamaso pa Mulungu. Mulungu amanyansidwa ndi makhalidwe otere.

**10. Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za munthu amene amati kuti ndiye mneneri kapena mbusa amene akhoza kuombeza maula?**
Yankho: Mulungu salolanso zimenezo. Aneneri kapena azibusa awa samvera Mulungu ndipo sitiyenera kuwamvera.

**11. Kodi tingaphatikize bwanji moyo wangwiro ndi Mulungu ndi kufunsira mizimu uphungu?**
Yankho: Sitingaphatikize izi. Mulungu atiletsa kufunsira kwa mizimu.

**12. Kodi mumayesa kuphatikiza kumvera Mulungu ndi kusamumvera pa nthawi imodzi?**
Yankho: aloleni kuyankha pa yekha. Ngati ife timatero kapena tinatero, tiyenera kuulula chimoli kwa Mulungu, kumupempha cikhululukiro ndi kuleka kucita tero.

- Werengani pamodzi <u>2 Mafumu 17.28-41</u> ndipo yankhani funso iri:

**13. Kodi ndi mafano otani amene amapezeka kwambiri m'dziko lathu ndi m'miyoyo yathu?**
Yankho: aloleni kuyankha pa yekha. Ciriconse cimene ciri cofunikira kwambiri kwa ife kuposa Mulungu yekha, ndico fano. Kwa ena cingakhale ndalama, mabanja awo, mbiri yao, thanzi lao kapena maganizo a mneneri. Ngakhale zinthu zabwino monga calichi zingakhale mafano ngati ziri zofunikira kwambiri kwa ife kuposa Mulungu. 1 Yohane 5.21.

*C. Yankho ya Mulungu ya kwa mdima – Yesu*

- Werengani pamodzi <u>1 Yohane 3.8</u> ndipo yankhani mafunso awa:

**14. Kodi Yesu anaononga bwanji nchito za mdyerekezi?**
Yankho: anatero mwa imfa yake ya pa mtanda.

**15. Kodi citanthauza ciani kwa ife kuti Yesu anaononga nchito za mdyerekezi?**
Yankho: akumbutseni za m'phunziro 2. Pamene chimo linalowa dziko lapansi, ubwenzi pakati pa Mulungu, ife, anthu ena ndi cilengedwe cina ndiwo woonongeka. Ndife anthu osokonezeka. Yesu anadza kukonza zonse. Yesu abwezeretsa anthu kwa Mulungu, kwa anthu ena, kwa cilengedwe komanso kwa iwo eni.

- Werengani pamodzi Akolose 2.15 ndipo yankhani mafunso awa:

**16. Kodi Yesu anacita ciani kwa maukulu ndi maulamuliro,ndiwo Satana ndi ziwanda?**
Yankho: anawabvula (analanda mwa mphamvu), anawaonetsera poyera ndi kuwagonjetsa.

- Werengani pamodzi <u>1 Yohane 4.4</u> ndi <u>2 Atesalonika 3.3</u> ndipo yankhani mafunso awa:

**17. Kodi munthu wotsatira Yesu ayenera kucita mantha ndi Satana? Cifukwa nciani mwayankha tero?**
Yankho: Iai. Satana angawabvutitse ndi kuwayesa, kotero iwo ayenera kukhala maso, koma mwa Kristu iwo ali otetezeka. Izi sizitanthauza kuti palibe coipa comwe cingawacitikire (akumbutseni aphunzi zomwe tinaphunzira m'phunziro 2 ndi 3).

**18. Kodi Mkristu wobadwa mwatsopano angakhale ndi ziwanda?**
Yankho: Iai. 1 Yohane 4.4 itiphunzitsa kuti Mzimu woyera ndi wamphamvu kuposa mizimu yonse: Kuukika kumathamangitsa mdima. Mkristu sangalamuliridwe ndi mizimu yoipa. Komabe, Mkristu wobadwa mwatsopano angabvutidwe ndi kuyesedwa (ndico cifukwa cake Mulungu atiuza kuti titsutse Satana – onani pansipa).

(Mudzazindikira kuti aphunzi angaleme pa kuphunzira zambiri. Aphunzitseni nyimbo kuti azitha kutsatira maphunziro ena onse a Baibulo)

*Ine ndine Kuunika kwa dziko lapansi.*
*Iye wonditsata Ine sayenda mu mdima.*
*Yesu, Yesu, ndiye Kuunika.*
*Bwerani kwa Yesu poti Iye ndi wabwino.*

*D. Kodi tingakane bwanji Satana?*

- Werengani pamodzi Mateyu 4.1-11 ndipo yankhani mafunso awa:

**19. Kodi Yesu anayankha bwanji Satana pamene Iye anayesedwa?**
Yankho: anauza Satana zimene ndi zolembedwa m'Baibulo komanso kuti Iye amvera Mulungu yekha (ndime za 4, 7 ndi 10).

**20. Kodi ife tiyenera kuyankha bwanji pamene tayesedwa?**
Yankho: tiyenera kucita cimodzimodzi monga Yesu anacita: kukana kucimwa ndi kumvera zimene Mulungu atiuza mwa Baibulo.

**21. Kodi tingakane bwanji Satana ngati si ndife okhazikika m'Baibulo?**
Yankho: sitingakane Satana ngati si ndife okhazikika m'Baibulo. Tiyenera kudziwa Baibulo kuti tikhoze kuzindikira macenjerero a Satana komanso kuti tidziwe zimene Mulungu afuna komanso kukana mayesero.

- Werengani pamodzi Yakobo 4.7-8 ndipo yankhani mafunso awa:

**22. Kodi cofunika nciani kuti munthu athe kukana mdyerekezi?**
Yanko: kukhala odzipereka ndi omvera Mulungu. Mulungu ali ndi mphamvu pa mdyerekezi (Zakariya 3.1-2)

- Werengani pamodzi Aefeso 6.10-18 ndipo yankhani mafunso awa:

**23. Werenganinso ndime ya 10. Kodi ndime iyi itiphunzitsa ciani pa kudalira pa azitsogoleri acipembedzo kapena anthu ena kumenya nkhondo yauzimu?**
Yankho: ndime iyi itiphunzitsa kuti tiyenera kukhala olimbika mwa Ambuye ndi mwa mphamvu yake. Sitingadalire pa wina aliyense kapena cina ciriconse koma pa Mulungu yekha.

**24. Werenganinso ndime ya 14. Fotokozani kuti cifukwa nciani kudziwa coonadi ca Mulungu ndi ca cipulumutso ndi kofunikira kwambiri.**
Yankho: ngati sitimvetsa kuti Mulungu ndani ndipo sitimvetsa kuti cipulumutso ndi cotani, tingasokeretsedwa mwamsanga. Mwachitsanzo: anthu ena aganiza kuti anthu a Mulungu opulumutsidwa ku macimo ao, adzakhala olemera (phunziro 3). Izi si zoona. Cipulumutso citanthauza kuyanjanitsidwa ndi Mulungu. Koma ngati muganiza kuti cipulumutso citanthauza kuti muyenera kukhala olemera koma simulo olemera, mudzayamba kukayikira ndipo pamenepo mudzakhala oyesedwa mwamsanga.

**25. Werenganinso ndime ya 15. Kodi citanthauzanji kukhala ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino?**
Yankho: citanthauza kukhala okonzeka kumvera ndi kuphunzitsa anthu ena coonadi.

**26. Werenganinso ndime ya 16. Kodi tingazime bwanji ziwembu za Satana?**
Yankho: mwa kukhulupirira m'mene Mulungu aliri komanso malonjezano ake.

**27. Werenganinso ndime ya 17. Kodi maganizo athu angatetezeke bwanji?**
Yankho: mwa ciyembekezo mwa Mulungu pa cipulumutso komanso mwa kusewenzetsa Baibulo.

**28. Werenganinso ndime ya 18. Tauzidwa kupemphera ndi kupirira. Kodi mumacita izi?**
Yankho: aliyense ayankhe pa yekha.

- Fulumizitsani aphunzi kudziwa ndi kumvera Yesu. Anthu ena angofuna Yesu kuti atetezedwe. Kwa iwo Yesu ndi njira ina yogwiritsira nchito mankhwala ocokera ku ng'anga. Yesu atetezadi, koma Iye ndiye woposa kungokhala Mtetezi. Iye ndi Mpulumutsi. Iye ndi Mfumu. Iye ndi Ambuye. Lapani macimo anu, khulupirirani Iye monga Mkhalapakati pakati pa Mulungu ndi ife ndipo Iye adzasamaliranso zina zonse.

## 4. Kupumula (10 minutes)

- Uzani gulu kuti liwerenge mpaka 20. Anthu ayenera kusinthana kunena nambala. Koma osati motsatira dongosolo lomwe akhala. Ngati anthu awiri alankhula nthawi imodzi, gulu liyenera kuyambanso kuwerenga.

## 5 . Zotsatira zake m'umoyo wa masiku onse (30 minutes)

- Werengerani aphunzi Aefeso 4.27. Tiyenera kuzindikira njira za Satana kuti timutsutse. Pali njira zambiri zomwe tingapatse Satana ndi ziwanda mpata m'miyoyo yathu:
  1. Pamene timakhala m'macimo. Satana afuna ife kupambukira Mulungu.
     a. *Satana ndi ziwanda angatiyese*. Mwacitsanzo, ngati munthu wina ataya ndalama za m'thumba mwake, tingayesedwe kuti tisakambepo koma kungodoba ndalamazo ndi kuzisewenzetsa. Kapena ngati wina atipatsa ndalama zoti tigone ndi mwamuna kapena mkazi kunja ku ukwati, Satana angatiuze kuti si chimo. Angatiuze kuti ndi njira yothandiza mabanja athu kuwagulira zosowa zao.

        *Bvuto lalikuli si mayesero koma mitima yathu yocimwa yofuna kugonja kwa mayesero (Yakobo 1.14). Sitingaike mlandu pa Satana pamene ticimwa.*

     b. *Ticimwa ndipo Satana ndi ziwanda zitilimbikitsa kutero.* Mwacitsanzo, tikafuna kudziwa cifukwa ca bvuto lina la m'moyo, tingapite ku African doctor. Satana adzaonetsetsa kuti tidzapeza thandizo. Motero tiganiza kuti kuombeza si chimo. Kapena ngati tikumva osasamalidwa m'ukwati, tingalake kupeza mwamuna kapena mkazi wina. Satana angabweretse anthu panjira pathu otipatsa cisamaliro capadera kuti potsiriza pake ticite cigololo.
  2. Pamene cinthu coipa cacitika, mosacedwapo tinena kuti cacitika cifukwa ca ciwanda. Mwacitsanzo, ngati ana akana kupita ku sukulu, makolo anganene kuti ndi cifukwa ca mzimu woipa wofuna kuononga tsogolo la anawo. Kapena wina akakwiya, tinganene kuti munthuyu ali ndi mzimu womumkwiyitsa. Koma Baibulo silinena kuti anthu ocimwa ali ndi mzimu ndipo silikamba kuti anthuwo afunika kumasulidwa. M'malo mwake, Baibulo liwauza kuti alape. Maganizo amenewa asonyeza kuti mizimu yoipa ili ndi malo m'maganizo mwathu. M'malo mwake, maganizo athu ayenera kudzazidwa ndi Mulungu ndipo maganizo athu ayenera kugwirizana ndi Baibulo.
  3. Ticita chidwi pa Satana ndi ziwanda. Satana ndi ziwanda akondwa ngati tiganizira ndi kulankhula za iwo. Sadandaula ngati ticita misonkhano yotulutsa ziwanda koma adandaula ngati anthu alapa ndi kukhulupirira Yesu pa cipulumutso. Musalemekeze ziwanda mwa kuononga ndalama kapena nthawi pa ciriconse cokhudzana nazo.

- Werengerani aphunzi Yohane 8.12. Fotokozani kuti anthu olamuliridwa ndi ziwanda, ayenera kudziwa Yesu. Yesu ndiye Kuunika komwe kugonjetsa mdima. Ayenera kudzipereka kwathunthu kwa Iye. Ayenera kuphunzitsidwa Baibulo ndiponso kupemphereredwa. Sitifunikira opempherera apadera kuti ticite zimenezo (onani phunziro

5). Sitinalamulidwa kuzitulutsa ziwanda. Mulungu adzathana ndi ziwanda kudzera m'ciphunzitso ca m'Baibulo ndi pemphero. Kumbukirani kuti Baibulo limacha ambiri omwe amatulutsa ziwanda, ocita kusayeruzika (Mateyu 7.21-23).

*Fotokozani izi pokhapokha ngati zafunsidwa:*
*Nthawi zambiri Luka 10.19 imagwiritsidwa nchito pofotokoza kuti Akristu ayenera kutulutsa ziwanda. Komabe, ngati tiwerenga mau ena anzake, tiona kuti lamuloli linali lapadera kwa anthu 70 okha. Ndi zoona kuti Akristu akhoza kutulutsa ziwanda, koma si nchito yao yaikulu. Nchito yao yaikulu ndi kulalikira Uthenga Wabwino wa Yesu amene anagonjetsa Satana.*
*Citsanzo cabwino ndi mpingo wa ku Efeso. Mpingowo unali wozunguliridwa ndi anthu okhala ndi mizimu yoipa (Macitidwe 19.11-19). Pamene Paulo anawafikira ndi Uthenga Wabwino, zozizwitsa zinacitika kuti zitsimikizire kuti mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu kuposa ya Satana. Koma pambuyo pake, mpingo utakhazikitsidwa, mpingo sunaitanidwe kuti uthane ndi ziwanda. M'kalata ya kwa Aefeso, Paulo anawauza kuti abvale zida za Mulungu (Aefeso 6.10-18) ndi kukhala ndi moyo woyera (Aefeso 4.27). ZIMENEZO ndi momwe mpingo ungatane ndi mizimu yoipa. Mulungu amachita zina zonse.*

## 6. Zolowapo (60 minutes)

- Uzani aphunzi kuti akhale m'magulu ang'ono ndipo perekani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti likambiranepo.

**1. Richard ndi Eunice**
Richard ndi Eunice ali ndi mwana wodwala kwambiri. Aganiza za kupempha thandizo kwa African doctor. Iye awauza kuti neba wao anapangitsa mwana wao kudwala. Neba uyo ndi wansanje ndipo afuna kuononga banja la Richard ndi Eunice.

1. Kodi Baibulo limati ciani za maula? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.
2. Kodi mungauze ciani Richard ndi Eunice? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.

**2. Elias ndi Cecilia**
Elias ndi Cecilia anali ndi mwana wao woyamba miyezi iwiri yapitayo. Dzina la mwanayo ndi Martha. Kuyambira masabata angapo Martha analira kwambiri makamaka usiku. Cecilia apempha upangiri kwa membala wa ku calichi. Membala wa ku calichi lao anena kuti mwanayo aona mzimu wa agogo ake omwe anamwalira. Cecilia alangizidwa kuti atenge masamba kucokera mumtengo winawake kuti asambitse mwana wao ndi masambawo. Cecilia anacita zomwe walangizidwa ndipo mwanayo asiya kulira.

1. Kodi muganiza ciani za mizimu ya akufa yoonekera kwa anthu amoyo? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.
2. Kodi ngati ndinu amene anapemphedwa uphungu pa nkhaniyi, munganene ciani?

**3. Dalitso and Chileshe**
Dalitso ndi Chileshe ali ndi ana 6 ndi adzukulu atatu. Akafunsidwa, iwo anena kuti sanakumanepo kwambiri ndi mizimu yoipa. Anthu ena a m'mudzi mwawo ali ndi nkhani zambiri zokhudza kubvutikidwa ndi mizimu yoipa, makamaka usiku. Afunsa Dalitso ndi Chileshe kuti zatheka bwanji kuti iwo sanakumanepo ndi zoterezi.

1. Kodi cifukwa cingakhale ciani cakuti Dalitso ndi Chileshe sanakumanepo kwambiri ndi mizimu yoipa?
2. Kodi inu mufuna kukhala ndi mtendere womwe Dalitso ndi Chileshe ali nao? Kodi tingapeze bwanji mtendere wotere? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.

**4. Alice**

Alice ndi mai wokalamba amene adaphunzitsidwa ndi agogo ake ndipo tsopano aphunzitsa adzukulu ake zimene iye yemwe adaphunzitsidwa. Tsiku lina, Alice akawerenga Baibulo lake, awerenga ndime iyi, 'Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva, kusiyana nao makhalidwe anu acabe ocokera kwa makolo anu' (1 Petro 1.18). Alice adzifunsa kuti ndime iyi itanthauzanji.

1. Perekani zitsanzo zitatu za nzeru zoipa ndi zopanda pake zimene tinalandira kwa makolo athu.
2. Kodi tingadziwe bwanji ngati zomwe tinaphunzitsidwa ndi makolo athu, ndi zazoona ndi za phindu?

**5. Donaria**

Donaria ndi membala wodzipereka ku calichi. Tsiku lina, azitsogoleri a calichi aganiza za kukonzekera usiku wa mapemphero (overnight prayer). Mbus awa ku Lusaka adzabwera ndi kumasula anthu ku ziwanda kuti anthuwo apeze mtendere m'miyoyo yao. Mbusayo ali ndi mbiri yabwino yothandiza anthu. Usiku umenewo, anthu ambiri asonkhana. Iwo aimba, apemphera ndipo ziwanda zambiri zatulutsidwa.

1. Kodi ndi ciani casowa m'nkhaniyi?
2. Kodi Donaria monga munthu wobadwa mwatsopano, angakhale ndi ciwanda? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.

**6. Timothy ndi Memory**

Mwana wao wa Timothy ndi Memory anamwalira pamene anakwanitsa caka cimodzi. Mabanja awo anawakakamiza kucita mwambo woletsa ana awo ena kufa ali aang'ono. Timothy ndi Memory anakana. Amakhulupirira Mulungu kuti adzawasamalira. Amawerenga Baibulo ndi kupemphera. Akacimwa alapa ndipo mwa cikhulupiriro adziwa Yesu. Tsiku lililonse amadalira pa Iye pa zonse ndipo amadzipereka kwa Iye. Saopa mdima. Akakomana ndi mabvuto, amakumbutsana kuti aliyense wotsatira Yesu, sayenda mumdima koma ali ndi kuunika kwa moyo (Yohane 8.12).

1. Kodi kudalira pa Yesu ndi kudzipereka kwa Iye kutanthauzanji?
2. Kodi kukhala ndi kuunika kwa moyo kutanthauzanji?
3. Ganizirani za anthu awiri a m'banja mwanu kapena m'mudzi mwanu omwe afunika kumva uthenga wa Yesu Kuunika. Pezani mpata wolankhula nao za Yesu.

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco (akumbutseni za m'phunziro la m'Baibulo, cifukwa ayenera kuphunzira kulumikiza Baibulo ndi miyoyo yao ya tsiku ndi tsiku).

**Richard ndi Eunice**

1. **Kodi Baibulo limati ciani za maula? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.**
   Yankho: Baibulo liletsa maula (mwacitsanzo Deuteronomo 18.10-12 ndi Levitiko 20.6).

2. **Kodi mungauze ciani Richard ndi Eunice? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.**
   Yankho: ayenera kupempha Mulungu thandizo, ayenera kumvetsetsa zimene Baibulo likamba za matenda ndi thanzi (onani phunziro 2), ayenera kufunafuna thandizo ku cipatala komanso kudzipereka kwa Mulungu. Yesaya 8.19.

**Richard ndi Cecilia**

1. **Kodi muganiza ciani za mizimu ya akufa yoonekera kwa anthu amoyo? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.**
   Yankho: ndi cosatheka kuti mizimu ya akufa ionekera kwa anthu amoyo. Mwacitsanzo Yobu 7.9-10 ndi Mlaliki 9.5-6.
2. **Kodi ngati ndinu amene anapemphedwa uphungu pa nkhaniyi, munganene ciani?**
   Yankho: osaganiza kuti wakufa akhoza kudzionetsera kwa mwanayo. Ana amalira pa zifukwa zambiri, mwacitsanzo kusakondwera ndi ulula. Pemphani Mulungu kuti akupatseni nzeru kuti mupeze coyambitsa bvutoli. Mpempheni kutonthoza mwanayo. Ngati kulira kupitirira, funani thandizo kwa madokotala kuti mudziwe ngati mwana ali ndi bvuto m'thupi.

**Dalitso ndi Chileshe**

1. **Kodi cifukwa cingakhale ciani cakuti Dalitso ndi Chileshe sanakumanepo kwambiri ndi mizimu yoipa?**
   Yankho: iwo ali otetezedwa ndi Yesu. Iwo ali anthu obadwa mwatsopano amene sapatsa mpata kwa Satana ndi ziwanda. Maganizo ao ndi odzazidwa ndi Mulungu. Ngati akomana ndi mabvuto, amasewenzetsa njira zololedwa ndi Mulungu kuti athetse mabvutowo.
2. **Kodi inu mufuna kukhala ndi mtendere womwe Dalitso ndi Chileshe ali nao? Kodi tingapeze bwanji mtendere wotere? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.**
   Yankho: aloleni ayankhe pa yekha. Tipeze mtendere mwa Yesu Kristu yekha: mtendere ndi Mulungu, anthu ena, cilengedwe ndi zina zonse (Aefeso 2.14). Lapani macimo anu ndipo dalirani pa Yesu yekha.

**Alice**

1. **Perekani zitsanzo zitatu za nzeru zoipa ndi zopanda pake zimene tinalandira kwa makolo athu.**
   Yankho: aloleni kupereka zitsanzo zosiyana-siyana. Ngati alephera kuyankha, apatseni zitsanzo zanu.
2. **Kodi tingadziwe bwanji ngati zomwe tinaphunzitsidwa ndi makolo athu, ndi zazoona ndi za phindu?**
   Yankho: nthawi zonse tiyenera kuona ngati zophunzitsidwa ndi monga za m'Baibulo. Tidziwa kuti Baibulo ndi loona ndi losasintha. 1 Yohane 4.1. 1 Atesalonika 5.21.
   Tiyenera nthawi zonse kuyesa ndi zomwe zili m'Baibulo. Tikudziwa kuti Baibulo ndi loona komanso losasinthika. 1 Yohane 4.1, 1 Atesalonika 5.21.

**Donaria**

1. **Kodi ndi ciani casowa m'nkhaniyi?**
   Yankho: Uthenga Wabwino wa Yesu Kristu: lapani macimo anu ndipo khulupiririrani Iye. Iye ndi wokwanira.

2. **Kodi Donaria monga munthu wobadwa mwatsopano, angakhale ndi ciwanda? Perekani yankho lanu kucokera m'ndime ya m'Baibulo.**
   Yankho: Iai. Mulungu sagawana zake ndi Satana. 1 Yohane 4.4, 1 Akorinto 6.19,Yohane 8.12.

**Timothy ndi Memory**

1. **Kodi kudalira pa Yesu ndi kudzipereka kwa Iye kutanthauzanji?**
   Yankho: kutanthauza kusiya mphamvu zathu ndi ulamuliro wathu: tibvomera kuti mphamvu zathu ndi zaucimo ndi zosakwanira. Kutanthauza kuyang'ana kotheratu kwa Iye pa zonse. Kutanthauza kudzipereka kwa Iye mwaufulu: ciriconse cimene Iye acita ndi cabwino.
   Dziwani kuti kungodziwa kuti Mulungu alipo ndi kuti Iye ndani, si zomwe Baibulo litanthauza ndi cikhulupiriro. Ngakhale ziwanda zimachita izi (Yakobo 2.19). Baibulo likanena za chikhulupiriro, litanthauza ubale pakati pa Mulungu ndi anthu komanso kumumvera Iye.
2. **Kodi kukhala ndi kuunika kwa moyo kutanthauzanji?**
   Yankho: kutanthauza kuunikiridwa ndi kupatsidwa mphamvu ndi Yesu. Kutanthauza kupulumutsidwa ku mdima wa uchimo ndi kusadziwa ndiponso kukhala ndi citsimikizo ca moyo wosatha (Macitidwe 26.18). Kutanthauza kutsatira ziphunzitso za Yesu mu zocita zathu za tsiku ndi tsiku (kumvera).
3. **Ganizirani za anthu awiri a m'banja mwanu kapena m'mudzi mwanu omwe afunika kumva uthenga wa Yesu Kuunika. Pezani mpata wolankhula nao za Yesu.**

## 7. Kutsiriza (5 minutes)

- Fupikitsani zimene zaphunzitsidwa lero: Mulungu ndi Satana ndi adani. Ndife oitanidwa kumvera Mulungu ndi kukana mdyerekezi. Timatero tikamvera Mulungu mosamalitsa. Aliyense womutsata ali ndi kuunika kwa moyo. Sitiyenera kuopa ziwanda ngati ndife opulumutsidwa ndi Yesu.
- Pempherani.

## Phunziro 5 Pemphero

<u>Zofunikira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

### 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro lotsiriza: Mulungu ndi Satana ndi adani. Ndife oitanidwa kumvera Mulungu ndi kukana mdyerekezi. Timatero tikamvera Mulungu mosamalitsa. Aliyense womutsata ali ndi kuunika kwa moyo. Sitiyenera kuipa ziwanda ngati ndife opulumutsidwa ndi Yesu.

### 2. Yankho la pemphero (20 minutes)
- Werengerani aphunzi ziganizo izi. Ngati abvomera ayenera kukweza manja ao. Ngati sabvomera sayenera kukweza manja ao. Aloleni kufotokozera mayankho ao ndipo kambiranani.
  1. **Mulungu amamva pemphero lirilonse.**
     Yankho: Zoona, Mulungu amamva mapemphero athu onse (Salimo 65.2). Samvera cabe mapemphero abwino opemphedwa ndi anthu opatulika. Amamva zonse zimene tikamba (Salimo 94.9).
  2. **Mulungu atipatsa ciriconse cimene tifuna ngati tipemphera.**
     Yankho: Si zoona. Atipatsa cabe ngati pemphero lathu lilingana cifuniro cace (1 Yohane 5.14).
  3. **Ngati Mulungu ayankha, amatipatsa pamenepo zimene tifuna.**
     Yankho: Si zoona. Nthawi zina Mulungu ayembekeza kuyankha. Nthawi zina sitipatsidwa konse yankho. Nthawi zina Mulungu ayankha m'njira ina. Tiyenera kukhulupirira Mulungu kuti acita zimene ziri zabwino koposa ndipo tiyeneranso kupemphera pemphero limene Yesu anapemphera, 'Kufuna kwanu kucitike' (Mateyu 26.42).
  4. **Ngati Mulungu sayankha, citanthauza kuti Mulungu ndi wosakhulupirika.**
     Yankho: Si zoona. Mulungu angasankhe kusayankha mapemphero athu cifukwa ca zifukwa zina, mwacitsanzo pakuti cimene tampempha sicitipindulitsa kapena pakuti tapemphera modzikonda (Yakobo 4.3). Tiyenera kumkhulupirira.
  5. **Kungobwereza-bwereza mau sikupangitsa mapemphero athu kuti ayankhidwedi.**
     Yankho: Zoona. Mulungu atiuza kusalankhula cinthu cimodzimodzi mobwereza-bwereza (Mateyu 6.7, Mlaliki 5.2).
  6. **Ngati Mulungu sayankha pemphero lathu, cabwino coposa ndico kuleka kupemphera.**
     Yankho: Si zoona. Mulungu atiuza kupemphera kosaleka (1 Atesalonika 5.17, Luka 18.1). Tiyenera kumyembekezera ndi kuyesa pemphero lathu ngati lilingana cifuniro ca Mulungu. Ngati siliri monga mwa cifuniro ca Mulungu tifunika kulisandutsa kuti lilingana cifuniro ca Mulungu.
  7. **Ngati tifuna Mulungu kuyankha mapemphero athu, tiyenera kufunsa anthu opatulika a Mulungu kutipempherera.**
     Yankho: Si zoona. Mapemphero a anthu ena sali ndi mphamvu kuposa mapemphero athu kuti Mulungu ayankhe. Baibulo litilimbikitsa kupempherana, koma si zoona kuti

anthu opatulika a Mulungu ali ndi cizolowezi cabwino kuposa anthu ena (onani munsi m'Kuwerenga Baibulo).

## 3. Kupemphera m'dzina la Yesu – Kuwerenga Baibulo (60 minutes)

- Werengani pamodzi 1 Timoteo 2.1-6 ndipo yankhani mafunso awa:

1. **Werenganinso ndime ya 5. Kodi m'umoyo wanu wa masiku onse munapempha thandizo kwa mkhalapakati kapena mlumikizi? Ngati inde, udindo wa munthuyo unali wotani?**
   Yankho: Udindo wa mkhalapakati ndi kuyanjanitsa anthu awiri kapena magulu awiri amene alimbana.
2. **Fotokozani njira imene Yesu ali Mkhalapakati.**
   Yankho: Yesu ndiye Mkhalapakati wa Mulungu ndi anthu. Mulungu ndi woyera, wopanda banga ndipo akuda macimo. Anthu onse acimwa. Cotsatira ndi cakuti anthu onse alimbana naye. Tidzalekanitsa kwa Mulungu ku Gehena muyayaya pokhapokha ngati macimo athu acotsedwa. Mwa cikondi ndi cisomo Mulungu anatuma Mwana wake Yesu kukhala Mkhalapakati wa Mulungu ndi anthu. Yesu anagwirizanitsa Mulungu ndi anthu mwa kumwalira pa mtanda kukhululukira macimo. Aliyense amene adalira pa Yesu yekha pa cikhululukiro cace ndiye woyanjanitsidwa ndi Mulungu. Kopanda Yesu kulibe ciyembekezo ca kwa ife kuti tilandiridwe ndi Mulungu. Yesu afuna kukhala Mkhalapakati wathu ndipo aliko.
3. **Kodi mufuna Yesu yekha kukhala Mkhalapakati wanu?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
4. **Kodi Mariya, aneneri, atumwi, azibusa kapena anthu ena angakhale pakati pa Mulungu ndi ife?**
   Yankho: Iai, kulibe anthu ena amene angakhale pakati pa Mulungu ndi ife koma Yesu Mwana wa Mulungu (Aefeso 2.18, Ahebri 7.25). M'Baibulo mulibe mpata wa wina aliyense kukhala mkhalapakati wathu. Sitifunika mkhalapakati pakati pa ife ndi Yesu pakuti Iye afuna kulandira wina aliyense wobwera kwa Iye (Yohane 6.37).
5. **Ndi cifukwa ciani tiyenera kupemphera m'dzina la Yesu nthawi zonse?**
   Yankho: Pakuti Yesu yekha ndiye Mkhalapakati wopangitsa ife ndi mapemphero athu kukhala zobvomerezeka pa maso pa Mulungu.

- Werengani pamodzi Aefeso 3.8-12 ndipo yankhani mafunso awa.

6. **Werenganinso ndime ya 12. Ndi cifukwa ciani Akristu aloledwa kupemphera mokhazikika mtima ndi moyandikira kwaufulu?**
   Yankho: Yesu ndiye cifukwa cakuti Akristu aloledwa kupemphera mokhazikika mtima ndi moyandikira kwaufulu. Mulungu akhoza kutimvera ndi kutiyankha cifukwa ca Yesu yekha. Ngati tikhulupirira Yesu, Mulungu sakhalabe kutali kwa ife koma ali pafupi pakuti Yesu anacotsa macimo athu otilekanitsa ndi Mulungu (Yesaya 59.2).
7. **Kodi kukhala ndi cokhazikika mtima ndi ciyandiko colimbika kutanthauzanji?**
   Yankho: Citanthauza kuti cifukwa ca Yesu tiloledwa kufika pafupi ndi Mulungu mosakayika. Osati cifukwa ca m'mene ife tiliri kapena cifukwa ca mapemphero athu, koma cifukwa ca Yesu ndife okhazikika mtima kuti Mulungu atimvera ndiponso kuti adzatiyankha.
8. **Werenganinso ndime ya 12. Kodi ndi anthu otani amene aloledwa kubwera pafupi pa mpando waufumu wa Mulungu mokhazikika mtima ndi moyandikira kwaufulu monga mwa ndime iyi?**
   Yankho: Aliyense amene ali ndi cikhulupiriro mwa Ambuye Yesu. Anthu awo ali oyanjanitsidwa ndi Mulungu kupyolera mwa Yesu. Kulibe anthu ena apadera amene ali

pafupi ndi Mulungu kuposa anthu ena. Okhulupirira onse ali ndi mpata wolowera umodzi wa kwa Mulungu cifukwa ca Yesu (Mateyu 7.8: *yense*). Sitiganiza bwino ngati tiganiza kuti anthu apadera a Mulungu ayankhidwa msanga kuposa anthu ena. Pa nthawi ya Cipangano Cakale Yesu asanabadwe, Mulungu anali ndi anthu ake apadera ndipo analankhula kupyolera mwa iwo. Koma Yesu atamwalira ndi kuuka kwa akufa, wokhulupirira aliyense ali ndi mpata wolowerera kwa Mulungu mwa Yesu mosacedwa.

- Werengani pamodzi Yohane 14.12-14 ndipo yankhani mafunso awa.

9. **Werenganinso ndime ya 14. Kodi kupemphera m'dzina la Yesu kutanthauzanji?**
   Yankho: Kutanthauza kupemphera m'mzimu umodzi wa Yesu. Kupemphera monga mwa cifuniro cace. Kufuna zimene Iye afuna. Sikutanthauza kupemphera ciriconse cimene tifuna ndi kutsiriza cabe mwa kunena 'M'dzina la Yesu. Amen'. Tiyenera kuganizirako mapemphero athu: kodi mapemphero athu ali monga mwa cifuniro ca Mulungu?' Pamene mupemphera, funsani Mzimu Woyera kukutsogolerani (Aroma 8.26).
10. **Anthu ena anena kuti tidzatukuka ndi kucita bwino nthawi zonse ngati tipemphera m'dzina la Yesu. Kodi tingayankhe bwanji anthu otere?**
    Yankho: Ngati tiwerenga ndime ya 12, tiona kuti Mulungu afuna anthu ake kucita zimene Yesu anacita: kutumikira ndi kulemekeza Mulungu mu zonse. Cifukwa cace si cabwino kupemphera 'm'dzina la Yesu' ngati timpempha galimoto, firiji, cokwezedwa ndi cina cotere pakuti zinthu izi siziri colinga cake ca Mulungu ca kwa ife. Colinga cathu ndico kulemekeza Mulungu mwa kukhala monga Yesu.

- Werengani Aefeso 2.13-22 ndipo yankhani mafunso awa.

11. **Werenganinso ndime ya 14. Kodi ndani amene atipatsa mtendere woona?**
    Yankho: Yesu.
12. **Werenganinso ndime ya 16. Kodi ndi m'njira yanji m'mene Yesu anabweretsa mtendere?**
    Yankho: Anabweretsa mtendere mwa kumwalira pa mtanda. Mwa kumwalira pa mtanda Iye anayanjanitsa anthu ocimwa ndi Mulungu. Anacotsa macimo (uchimo ndiwo udani).
13. **Werenganinso ndime za 18, 19 ndi 20. Kodi cipatso cimodzi ca imfa ya Yesu ndico ciani monga mwa ndime izi?**
    Yankho: Ndico cakuti iwo amene ali mwa Yesu ali pafupi ndi Mulungu.
14. **Kodi tifunika anthu ena ake kucita cinthu kuti Mulungu akhoza kukhala pafupi nafe ndi kutidalitsa?**
    Yankho: Iai sitifunika anthu ena ake. Ticimwa ngati tiganiza kuti tifunika munthu wina kucotsa linga lokhala pakati pa Mulungu ndi ife. Kuganiza kuti tifunika wina kupatula kwa Yesu ndiko kupembedza mafano. Tiloledwa kufunsa anthu ena kutipempherera koma osaganiza kuti Mulungu ali kutali kwambiri kotero kuti tifunika munthu wina kupatula kwa Yesu kuti Mulungu angakhale pafupi ndi ife. Linga lokhala pakati pa Mulungu ndi ife ndilo uchimo ndipo Yesu yekha akhululukira macimo. Ngati tili mwa Yesu, ndife pafupi ndi Mulungu. Ndife a banja la Mulungu cifukwa ca Yesu (ndime ya 19).

## 4. Kupumula (10 minutes)

- Ngati aphunzi afuna, aloleni kusewera sewero pa nthawi yopumula. Mphunzi m'modzi ayamba sewero ndi kutsiriza ciganizo ici: 'Ndipita pa ulendo ndipo ndinyamula…'. Mwacitsanzo: 'Ndipita pa ulendo ndipo ndinyamula zobvala'. Munthu wina ayenera kunenanso cimene cakambidwa ndipo ayenera kuonjezera. Mwacitsanzo, 'Ndipita pa ulendo ndipo ndinyamula zobvala ndi nkhuni'. Munthu wina ayenera kunenanso ciganizo ico ndi kuonjezeranso. Pamene alephera kukumbukira zimene zakambidwa, mungayambenso konse sewero.

## 5. Mapemphero athu (20 minutes)

*Inu aphunzitsi mufunika kumvetsetsa ndi kukumbukira kuti anthu amapemphera m'njira zosiyanasiyana. Mulungu ayang'ana m'mtima. Ngati aphunzi akufunsani za kukweza manja kapena za kuyendayenda pa kupemphera, afunseni, 'Ncifukwa ciani mumacita tero?' Nchito yanu ndi kupangitsa anthu kuganizirako mapemphero athu ngati muli ulemu.*

- Funsani aphunzi ngati anapita konse kwa chief ndi pempho. Afunseni za cofunikira ca kuonetsa ulemu pa kukomana ndi chief.
- Fotokozani kuti pamene tipemphera tidza pa mpando wacifumu woyera wa Mulungu. Ndico colowa codwabwitsa. Si anthu onse amene aloledwa kuyendera pulezidenti wa ku Zambia koma anthu onse aloledwa kudza kwa Mulungu mwa pemphero. Mulungu ayenera ulemu wonse pamene tilankhula kwa Iye.
- Funsani aphunzi kuti tingaonetse ulemu m'njira zotani pamene tipemphera:
    - Timacita ciani ndi manja athu? Cifukwa nciani timacita tero?
    - Timacita ciani ndi miyendo/mapazi athu? Cifukwa nciani timacita tero?
    - Timakamba bwanji? Cifukwa nciani timacita tero?
- Malizitsani pa kufotokozera m'mene tingapatse ulemu kwa Mulungu. Mwacitsanzo m'njira izi:
    - **Titseka maso athu** kuti tisasokonezeke ndi munthu wina aliyense koma tiganizireko Mulungu yekha. Osalola wina aliyense kapena cinthu ciriconse kukusokonezani. Yesani kupeza malo kumene kuli bata. Pa kupemphera m'calichi, osalola anthu kulowamo kapena kucokamo pa nthawi yopemphera.
    - **Tiika manja athu pamodzi** kuonetsa kuti tilibe mphamvu ndi nzeru koma tidalira pa Mulungu.
    - Lankhulani **mwaulemu**. Si cabwino kukuwira chief. Si cabwinonso kukuwira Mulungu. <u>Genesis 18.27</u>.
    - Lankhulani **modzicepetsa**. Sitingauze chief kucita ciani. Sitingauzenso Mulungu kuti ayenera kucita ciani. Timlemekeza ndi kumpempha zosowa zathu. Mkhalidwe wabwino ndi kugwada pansi pa kupemphera. <u>Salimo 123.2, Yesaya 57.15</u>.
    - Lankhulani zocokera **mwa mtima mwanu**. Osangobwereza mau amene anthu ena akamba pamene apemphera. Kambani kwa Iye ndi mau a inu mwini ocokera m'mtima mwanu. Tiloledwa kupemphera Pemphero la Ambuye koma ngati sitimvetsa citanthauzo cace ndipo sitibvomera konse, kupemphera Pemphero la Ambuye kuli kopanda tanthauzo. <u>Salimo 62.8</u>
    - Khalani **osanamizira**. Sitikhoza kunamizira Mulungu. Adziwa zonse. Ngati muuza Mulungu kuti mwadza modzicepetsa pa maso pake komabe muli odzikudza cifukwa ca m'mene muliri kapena cifukwa ca pemphero lanu, muli kunamiza. Mau cabe sakondweretsa Mulungu. Khalani osanama. <u>Ahebri 4.13, Mateyu 15.7 ndi 8</u>.

- **Khulupirirani** kuti Mulungu atimvera ndiponso kuti adzatiyankha m'njira yabwino koposa pakuti adziwa zabwino zoposa. Mkhulupirireni ndipo yembekezerani molakalakira yankho lake. Ahebri 11.6, Yohane 4.24.

## 6. Zolowapo (30 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono ndipo patsani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti akambireko.

**Colowapo 1 Edson**

Edson anali kutsuka magalimoto kwa zaka zambiri. Caka cino iye anakwaniritsa kupeza laisensi yoyenera kuyendetsa galimoto koma abvutika kupeza nchito. Anali kupemphererapo koma bvuto lake likalibe kuthetsedwa. Usiku wina atumira foni mneneri amene alalikira ndi kupemphera ku wailesi. Edson afotokozera mneneri bvuto lake. Mneneri ayankha, 'Ndakutsegulirani citseko m'dzina la Yesu'.

1. Patsani zitsanzo ziwiri za mapemphero anu osayankhidwa.
2. Kodi mukumva bwanji za njira imene mneneri anayankha?
3. Kodi mungalangize ciani Edson?

**Dorika**

Dorika ndiye membala wa ku calichi. Nthawi zambiri iye auzidwa kupemphera. Anthu akonda njira yake ya kupemphera. Dorika sacita manyazi ndipo akamba mokuwa. Nthawi zina akwaniritsa ngakhale kupfuula. Auza Mulungu kuwapatsa kukolola kwabwino m'dzina la Yesu. Atapembedza mamembala a mpingo auza Dorika kuti pemphero lake linali lamphamvu ndiponso kuti pempherolo lidzayankhidwadi. Awafunsa kuwaphunzitsa kupemphera cimodzimodzi kuti Mulungu awapatse ciriconse cimene iwo afuna.

1. Kodi mudziwa anthu amene akwaniritsa kupemphera mwamphamvu?
2. Kodi muganiza kuti pemphero lamphamvu ndi lotani?
3. Kodi mukumva bwanji za kuitanitsa ciriconse cimene tifuna Mulungu kutipatsa?

**Nelson**

Nelson ali ndi zaka 35. Ndi wodwala nthawi yaitali. Nthawi zambiri iye akosomola ndipo ali wofooka. Nelson anayesa kupeza yankho ku ng'anga koma bvuto lake silinathetsedwe iye angakhale analipira zambiri. Anthu anampempherera koma apezekabe ndi bvuto lake. Tsiku lina Nelson amvera ku wailesi. Mneneri anena kuti anthu onse obvutika ayenera kubwera ku calichi ina yake ku Petauke kuti anthuwo apatsidwe pepala ndi pempho lao. Akacita tero Mulungu adzathandiza. Nelson asinkhasinkha kupeza njira yoyendera mneneri pakuti cioneka monga mneneriyo akhoza kuciritsa anthu.

1. Kodi muganiza ciani za anthu okamba kuti Mulungu aciritsa cabe mwa munthu wina wake kapena calichi cina cake?
2. Kodi ngati ndinu Nelson mufunika kucita ciani?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco.

**Edson**

1. **Patsani zitsanzo ziwiri za mapemphero anu osayankhidwa.**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi mukumva bwanji za njira imene mneneri anayankha?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao.
   - Fotokozani kuti mneneri sanafunse kalikonse kwa Mulungu, koma analamula citseko kutsegulidwa. Sitikhoza kupangitsa Mulungu kucita cimene tifuna. Mneneri sanaonetse kudzicepetsa ndi kudalira pa Mulungu.
   - Akumbutseni za m'Kuwerenga Baibulo: sitiyenera kugwiritsa nchito moipa dzina la Yesu kudzikhutitsa ndi zilakolako zokhudza za dziko lapansi.

3. **Kodi mungalangize ciani Edson?**
   Yankho: Palibe bvuto ngati tipempha anthu ena kutipempherera. Koma osaganiza kuti anthu ena ali ndi cizolowezi cabwino ca kwa Mulungu kuposa ife ngati ndife Akristu. Pemphani Mulungu modzicepetsa ndipo mkhulupirireni kuti adzayankha mwanzeru. Ici citanthauza kuti Mulungu angakane kuyankha kapena kuyankha m'njira ina yosayembekezeka.

**Dorika**

1. **Kodi mudziwa anthu amene akwaniritsa kupemphera mwamphamvu?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha.
2. **Kodi muganiza kuti pemphero lamphamvu ndi lotani?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao. Mangirirani pa kunena kuti mulibe mphamvu mwa pemphero lathu kapena mwa njira yopemphera koma mwa Yesu. Iye ndiye wopangitsa mapemphero kuti ayankhidwe. Cifukwa cace tipemphera m'dzina la Yesu. Mulungu amvera ndi kuyankha ndithu mapemphero eni-eni osamveka ndi anthu (1 Samueli 1).
3. **Kodi mukumva bwanji za kuitanitsa ciriconse cimene tifuna Mulungu kutipatsa?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao. Tiloledwa kufunsa Mulungu ciriconse cimene tisowa ndiponso kumuuza zobvuta zathu zonse. Akumbutseni za cofunikira ca kukhala odzicepetsa ndi osanamizira. Akumbutseninso kuti colinga cathu si kukhala ndi moyo wolimba nthawi zonse koma kukhalira m'cikhulupiriro, kukondwera m'zobvuta ndi kudzipereka kwa Mulungu.

**Nelson**

1. **Kodi muganiza ciani za anthu okamba kuti Mulungu aciritsa cabe mwa munthu wina wake kapena calichi cina cake?**
   Yankho: Aloleni kuuzana maganizo ao. Akumbutseni kuti aneneri a m'Baibulo sanakope anthu kubwera kwa iwo mwini koma kwa Mulungu. Ngati tiganiza kuti Mulungu angagwire nchito cabe mwa anthu ake apadera, timlembera malire ndipo kumlembera malire ndiko kumnyazitsa.
2. **Kodi ngati ndinu Nelson mufuna kucita ciani?**
   Yankho: Aloleni kuuzana mayankho. Nelson ayenera kumvetsa kuti Baibulo litilimbikitsa kupempherana. Ayenera kumvetsa kuti mphamvu siili mu mneneriyo. Ayenera kufufuza ngati mneneriyo aphunzitsa ndi kucita monga mwa m'Baibulo (phunziro 5).

## 7. Kutsiriza (5 minutes)

- Fupikitsani zimene zaphunzitsidwa lero: kupemphera ndiko udindo ndi umwayi wa Mkristu aliyense. Tiyenera kuzindikira kupemphera ciani ndi m'njira yotani. Kupemphera kukhudza <u>ubwenzi wathu</u> ndi Mulungu.
- Pempherani.

## Phunziro 5 Coonadi ndi cinyengo

Zofunikira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

### 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro lotsiriza: kupemphera ndiko udindo ndi umwayi wa Mkristu aliyense. Tiyenera kuzindikira kupemphera ciani ndi m'njira yotani. Kupemphera kukhudza ubwenzi wathu ndi Mulungu.

### 2. Nkhani (20 minutes)
- Werengerani aphunzi nkhani iyi.

  Jairos ali ndi zaka makumi atatu (30). Akhala ndi banja lake ku mudzi waung'ono. Nthawi zambiri pamene iye anali wacicepere, iye anapita ku chire ndi abwenzi ake. Anasewerako nthawi zambiri. Nthawi zina iwo anakwaniritsa kupeza zipatso zolamitsa ku chire.

  Tsiku lina Jairos afuna kubwerera ku chire kumene iye ankasewera pamene anali wacicepere. Kunatenga nthawi kucokera pa nthawi imene iye anapitako. Ngati zipatso izo zipezekeko! Jairos akaganizira cabe zipatso izo, iye akumva njala. Kupeza zipatsozo zokoma ndi zolamitsa kudzakhala bwino kwambiri. Alakalaka kupatsanso banja lake zipatso izo!

  Uko Jairos apita. Ayendako kanthawi. Cioneka kuti zipatso zimene iye ankadya tsono kulibe. Pepani kwambiri. Analakalaka kukondweretsa kwambiri banja lake powadyetsa zipatso izo zolamitsa.

  Jairos apotoloka kupita kunyumba. Pa nthawi iyo mwadzidzidzi aona mtengo wobala zipatso izo zokoma ndi zolamitsa! 'Izo ndi zimene ndafuna', Jairos aganiza. Athamanga ku mtengo niyamba kuthyola zipatso. Atenga zonse zimene akhoza kusunga m'matumba ndi malaya ake. Pa kuyenda kunyumba Jairos ayenda moseka. Tsiku labwino!

  Atafika kunyumba Jairos aonetsa banja lake zipatso zimene abwera nazo. Onse alemekeza Jairos pa kupeza zipatso zokoma ndi zolamitsa. Mosacedwa iwo ayamba kudya zipatsozo. Tsiku iri ndi tsiku labwino kwa iwo onse.

  Koma tsiku lina zonse zioneka zosiyana. Kulibe munthu amene akondwera. Onse amene anadya zipatso samvera bwino. Mamembala ena a m'banja adwala kwambiri ndipo angafune kupita ku cipatala. Kuoneka ngati Jairos analakwa: anaganiza kuti anapeza zipatso zokoma ndi zolamitsa koma mosazindikira iye anathyola zipatso zokhoza kupha.

  Kuli kusiyana kwa cakudya colamitsa ndi cakudya cokhoza kupha. Kulinso kusiyana kwa ciphunzitso coona ndi ciphunzitso conyenga. Baibulo likamba kuti tiyenera kumvera ciphunzitso colamitsa (Tito 2.1). Ngati timvera ciphunzitso conama, miyoyo yathu yauzimu idzaonongeka. Cimodzimodzi monga thanzi yabwino ya Jairos inaonongedwa ndi zipatso zokhoza kupha.

- Kambiranani mafunso awa:
  1. **Fotokozani zimene zinacitika m'nkhani.**
     Yankho: Aloleni aphunzi kuuza nkhani mofupikitsa.
  2. **Kodi tingaphunziremo ciani m'nkhani iyi?**
     Yankho: Tifunika kudziwa kusiyana kwa ciphunzitso coona ndi ciphunzitso conama. Tifunika kuyesa zimene taphunzitsidwa (1 Atesalonika 5.21). Ciphunzitso conama cingaoneke cabwino ndipo cinganamizire anthu ambiri.
  3. **Kodi tingasiyanitse bwanji ciphunzitso coona ndi conama?**
     Yankho: Kudziwa kusiyana kungabvute kwambiri. Cifukwa cace tiyenera kuyesa ziphunzitso zonse. M'Kuwerenga Baibulo tidzaphunzira kusiyanitsa aneneri/azibusa oona ndi onama ndi ziphunzitso zao.

## 3. Kusiyanitsa zonyenga ndi zoona – Kuwerenga Baibulo (60 minutes)

- Fotokozani kuti kusiyanitsa zonyenga ndi zoona kungakhale kobvuta. Cifukwa cace nthawi zonse tifunika Mulungu yemwe kutitsogolera. Pemphani Mulungu thandizo lake ndi nzeru zocokera kwa Iye. Kuonjezera apa kuli mafunso amene tingafunse kuti tithandizike pa kusiyanitsa zoona ndi zonyenga. Tidzaganizirako mafunso awa m'Kuwerenga Baibulo.

**Funso 1. Kodi abusa/aneneri ndi ziphunzitso zigwirizana ndi zimene Mulungu anabvumbulutsa m'Baibulo?**

- Werengani pamodzi Yeremiya 35.15, 1 Akorinto 14.3 ndi Marko 1.15 ndipo yankhani mafunso awa.
  1. **Kodi udindo waukulu wa munthu wolankhula m'malo mwa Mulungu ndiwo wotani?**
     Yankho: Kumangirira anthu, kulimbikitsa ndi kusangalatsa.
  2. **Kodi ndi mau otani omwe ayenera kunenedwa kwa anthu?**
     Yankho: Lapani macimo anu ndipo khulupiriráni Yesu kuti muyanjanitsidwe ndi Mulungu.
  3. **Kodi kulapa ndi kotani?**
     Yankho: Kutanthauza kumva cisoni pa macimo athu, kusiya macimo athu ndi kupempha Mulungu cikhululukiro.
  4. **Kodi uthenga wabwino ndi wotani?**
     Yankho: Uthenga wabwino wonse ndi wa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu amene anadza kufera anthu ocimwa nauka kwa akufa. Aliyense amene adzipereka kwa Yesu yekha ndi kudalira pa Iye, alandira cikhululukiro ca macimo ndipo ayanjanitsidwa ndi Mulungu. Uthenga wabwino ndi wakuti sitiyenera kuthandiza Mulungu kuti akhoza kutipulumutsa pakuti Yesu anacita ndi kutsiriza zonse! Uthenga wabwino ndi wokhudza Yesu, osati cuma, madalitso, thanzi kapena cinthu cina ciriconse cimene tingakonde.

- Werengani Agalatiya 1.9 ndi Macitidwe 17.10-11 ndipo yankhani mafunso awa.
  5. **Kodi cotsatira ndi ciani ngati munthu aphunzitsa mosiyana ndi za m'Baibulo (Mau a Mulungu)?**
     Yankho: Munthuyo sanatumidwe ndi Mulungu ndipo Mulungu atemberera anthu otero. Iwo amene azindikira kuti anaphunzitsa ziphunzitso zonyenga, ayenera kulapa ndi kupempha Mulungu cikhululukiro. Afuna kukhululukira!
  6. **Ndi cifukwa ciani Aberea analemekezedwa (Macitidwe 17.11)?**
     Yankho: Iwo anayesa ziphunzitso zimene anamva ngati zinali monga mwa Mau a Mulungu. Ifenso tiyenera kuyesa ziphunzitso ngati zili monga mwa m'Baibulo. Zonse zimene zitsutsa ndi Baibulo ziyenera kukanidwa.

**Funso 2. Kodi munthu wophunzitsa aliri monga za m'Baibulo?**

- Werengani pamodzi Mateyu 7.15-20 ndi Tito 1.6-9 ndipo yankhani mafunso awa.

7. **Werenganinso Mateyu 7.20. Kodi ndime iyi itanthauza ciani?**
   Yankho: Itanthauza kuti anthu a Mulungu azindikirika ndi zipatso zao. Anthu a Mulungu apatsa zipatso zabwino (makhalidwe abwino ndi ziphunzitso zabwino) ndipo ena sapatsa zipatso zabwino. Tiyenera kuwayesa mwa kuyang'anira zipatso zao.
8. **Kodi mudziwa atsogoleri a mipingo amene abala zipatso zopezeka m'Tito 1.6-9?**
   Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha. Baibulo likamba za zipatso zinanso m'ndime zina, mwacitsanzo m'1 Timoteo 3.2 ndi 3.

**Funso 3. Kodi ulosi wao ucitikadi?**

- Werengani Deuteronomo 18.22 ndi Yeremiya 28.9 ndipo yankhani mafunso awa.

9. **Kodi tiyenera kukhulupirira wina aliyense amene anena kuti akhoza kunenera za kutsogolo m'dzina la Ambuye?**
   Yankho: Iai, osati wina aliyense. Tiyenera kuonetsetsa bwino ngati zonenedwa za kutsogolo zicitika. Ngati sizicitika citanthauza kuti munthuyo sanalankhule m'dzina la Mulungu. Munthuyo anangonena zimene anthu anakonda kumvera kapena zimene iye anaganiza kuti zingacitike.
10. **Aneneri onyenga anganene kuti ulosi wao sunacitike cifukwa ca mphamvu ina yake yauzimu imene inawaletsa. Kodi mukumva bwanji za ici?**
    Yankho: Mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu kuposa mphamvu ya munthu wina aliyense. Ngati Mulungu akamba kuti cidzacitika cidzacitika ndithu.

**Funso 4. Kodi munthuyo aphunzitsa ndi kukhala pa zoona?**

- Werengani pamodzi 2 Timoteo 4.3-4 ndi 2 Petro 1.16 ndipo yankhani mafunso awa.

11. **Werenganinso 2 Timoteo 4.4. Kodi kulubza dala pacoonadi kutanthauza ciani?**
    Yankho: Kutanthauza kukhala osafuna kumva ndi kumvera coonadi koma kufufuza cinthu cina. Kutanthauzanso kusiya Uthenga Wabwino wa Yesu Kristu.
12. **Kodi kupatukira kutsata nthanu zacabe kutanthauza ciani?**
    Yankho: Kutanthauza kumva ndi kumvera ciphunzitso cimene siciri coona konse. Kukonda nkhani kuposa coonadi.
13. **Werenganinso 2 Petro 1.16. Kodi tidziwa bwanji kuti sititsata nkhani zacabe koma coonadi ca Mulungu?**
    Yankho: Zonse zolembedwa m'Baibulo zinacitika ndithu. Kuli anthu ambiri amene ali mboni. Cifukwa cace tidziwa kuti Uthenga Wabwino wa Yesu Kristu si nkhani cabe, koma coonadi ca Mulungu.

- Mangirirani pa kunena kuti tikafuna kuyesa munthu kapena ciphunzitso, tiyenera kuyankha mafunso awa onse anai. Mafunsawa onse anai ayenera kubvomerezedwa tisanayese munthu kapena ciphunzitso kukhala wolamitsa kapena colamitsa. Ngati tizindikira kuti munthu ndi wonyenga kapena ciphunzitso ndi conyenga, tiyenera kuleka kumvera. Tsatirani zolongosoka!

## 4. Kupumula (10 minutes)

- Lolani aphunzi kudzikonzekera kulemba mayeso.

## 5. Mayeso (45 minutes)

- Kulemba mayeso ndi kosakakamiza. Ngati mufuna aphunzi kulemba mayeso, tengerani mayeso amene apezeka pa tsamba lotsiriza la buku liri musanayambe kuphunzitsa kapena awerengereni mafunso kapena lembani mafunso pa bolodi.
- Aloleni aphunzi kulemba mayeso.
- Congani mayeso. Mayankho abwino ali conco:

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 A | 2 B | 3 A | 4 B | 5 A | 6 B | 7 C | 8 B | 9 C | 10 B |
| 11 A | 12 B | 13 B | 14 B | 15 C | 16 A | 17 C | 18 A | 19 C | 20 A |

## 6. Kutsiriza

- Yamikirani aphunzi pa kubwera ku maphunziro.
- Alimbikitseni kuwerenga bwino Baibulo kudziwa coonadi ca Mulungu. Pemphani Mulungu kukupatsani nzeru ndi thandizo. Iye afuna kupatsa.
- Pempherani.

# Mayeso Umoyo Wacikristu

Dzina……………………………………………………………..

Stephanos

1. **Kodi buku loyamba la m'Baibulo limene litiphunzitsa za kulengedwa kwa zonse ndilo ciani?**
   - A. Genesis
   - B. Cibvumbulutso
   - C. Mateyu

2. **Kodi mabuku anai a Uthenga Wabwino wa m'Cipangano Catsopano atiphunzitsa ciani?**
   - A. Atiphunzitsa kuti tifunika kucita zabwino kuti tilowe Kumwamba.
   - B. Atiphunzitsa za Yesu pamene Iye anali pa dziko lapansi.
   - C. Atiphunzitsa za kulalikira Uthenga Wabwino.

3. **Kodi aneneri a m'Cipangano Cakale anaphunzitsa za ciani?**
   - A. Za Mulungu, macimo ndi cipulumutso kupyolera mwa Mpulumutsi wolonjezedwa (Yesu).
   - B. Za madalitso ndi kupindula.
   - C. M'Cipangano Cakale sitiwerengamo za aneneri.

4. **Buku la mneneri Yesaya linalembedwa Yesu asanabadwe.**
   - A. Bodza
   - B. Zoona

5. **M'Cipangano Cakale tiwerenga za Yesu Mpulumutsi wolonjezedwa.**
   - A. Zoona
   - B. Bodza

6. **Kodi ndi dalitso lotani limene Cipangano Catsopano cilankhulirako kwambiri?**
   - A. Maciritso
   - B. Cikhululukiro ca macimo
   - C. Kupindula

7. **M'Mateyu 6.33 tiwerenga kuti, Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu'. Kodi ndime iyi itanthauza ciani?**
   - A. Itanthauza kuti tikakhulupirira Mulungu tidzakhala ndi zonse zimene tifuna.
   - B. Itanthauza kuti anthu opezeka m'Ufumu wa Mulungu ali ndi cuma kuposa anthu ena.
   - C. Ithanthauza kuti tikakhulupirira Mulungu sitiyenera kudera nkhawa pa zofunikira za masiku onse.

8. **Mulungu afuna Mkristu aliyense kulemera.**
   - A. Zoona
   - B. Bodza

9. **Kodi kulemera koona kutanthauza ciani monga mwa m'Baibulo?**
   - A. Kutanthauza kulemera kwambiri kotero kuti sitiyenera kudera nkhawa pa cakudya ndi zobvala.
   - B. Kutanthauza kuti tikhoza kugula ciriconse cimene tifuna.
   - C. Kutanthauza kukhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Yesu Mpulumutsi.

10. **Kodi colinga ca imfa ya Yesu pa mtanda cinali cotani?**
    - A. Colinga ndi cakuti anthu ake akondwera m'miyoyo yao.
    - B. Colinga ndi cakuti ayanjanitse Mulungu ndi anthu ocimwa mwa kucotsa macimo ao ndi kuwapangitsa kukhala oyera pa maso pa Mulungu.
    - C. Imfa ya Yesu inali kopanda colinga.

**11. Kodi tiyenera kucita ciani pamene tadwala?**

- A. Tiyenera kupemphera, kudalira pa Mulungu ndi kufunafuna thandizo mosagwiritsa nchito njira yosaloleka.
- B. Tiyenera kufufuza kuti mzimu wotipangitsa kudwala ndiyo yotani.
- C. Sitiyenera kucita cinthu ciriconse pakuti Mulungu ndiye Mlengi wathu.

**12. Mulungu afuna Mkristu aliyense kulandira maciritso.**

- A. Zoona
- B. Bodza

**13. Kodi mwini cuma wa m'Baibulo anasauka m'njira yanji iye angakhale anali ndi cuma?**

- A. Analibe abwenzi kapena banja.
- B. Sanali wokonzeka kukomana Mulungu pamene iye anamwalira.
- C. Kukolola kwake sikunali kwabwino konse.

**14. Kodi Yesu ananena ciani?**

- A. Iye wonditsata Ine angapemphe thandizo kwa ang'anga ena.
- B. Iye wonditsata Ine sadzayenda mu mdima.
- C. Iye wonditsata Ine sadzakomana ndi mabvuto.

**15. Kodi ndani amene akhoza kukhala pakati pa Mulungu ndi ife?**

- A. Kulibe amene akhoza kukhala pakati pa Mulungu ndi ife.
- B. Aneneri, azibusa, atumwi ndi anthu ena amene akhala pafupi ndi Mulungu.
- C. Yesu yekha akhoza kukhala pakati pa Mulungu ndi ife.

**16. Kodi cifukwa nciani kuti tiyenera kupemphera nthawi zonse m'dzina la Yesu?**

- A. Pakuti Yesu yekha akhoza kupangitsa mapemphero kuti alandiridwe ndi Mulungu.
- B. Pakuti ngati sitipemphera m'dzina lake sitidzapatsidwa zimene tifuna.
- C. Pakuti azitsogoleri a mpingo apemphera m'dzina la Yesu.

**17. Aefeso 3.12 ikamba kuti, 'Amene tiri naye cokhazikika mtima ndi ciyandiko colimbika, mwa cikhulupiriro ca pa Iye'. Kodi ndani amene ali ndi ciyandiko ca kwa Mulungu monga mwa ndime iyi?**

- A. Anthu apadera a Mulungu cabe amene akhala pafupi naye kuposa anthu ena.
- B. Anthu a m'Cipangano Cakale amene anapereka nsembe.
- C. Aliyense amene akhulupirira Yesu Mpulumutsi.

**18. Kodi tinaphunziramo m'nkhani ya Jairos?**

- A. Tiyenera kumvera ciphunzitso colamitsa kuti tikhale amphamvu m'uzimu.
- B. Kuganizira kwambiri za kumbuyo si kwabwino koma tiyenera kuyang'ana m'tsogolo.
- C. Tiyenera kusamalira mabanja athu.

**19. Kodi ndi funso lotani limene <u>silithandiza</u> kusiyanitsa azitsogoleri oona ndi onyenga?**

- A. Kodi abusa/aneneri ndi ziphunzitso zigwirizana ndi zimene Mulungu anabvumbulutsa m'Baibulo?
- B. Kodi munthu wophunzitsa aliri monga za m'Baibulo?
- C. Kodi mtsogoleri ali ndi anthu ambiri omtsata?

**20. Kodi tifike bwanji Kumwamba?**

- A. Tidzafika Kumwamba ngati talandira Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wathu.
- B. Tidzafika Kumwamba ngati ticitira zabwino anthu ena.
- C. Tidzafika Kumwamba ngati ticita zimene azitsogoleri a mipingo atiuza.

## Zikomo!